

NJIRA YA KUMOYO WOSATHA

- Si chuma, mphamvu, kapena chikondi cha umunthu zomwe munthu amazilakalaka. Chosowa chachikuru ndicho kubvomerezeka ndi Mulungu.
- Mankhwala, kuledzera, kusuta, mkwiyo, kunenepa kuposera muyeso, nkhawa zachiritsidwa kwa myaya-Tifufuze chomwe chazithetsa.

MAU OYAMBA

Kukanakhala kuti ziphunzitsa za mau a Mulungu zinaloredwa kulumulira ndi kuchita chikoka m'moyo wa mwamuna kapena mkazi ali yense, ndipo malingaliro ndi mtima zinagonja pansu pa mphamvu ya Mulungu, zoipa zonse zomwe zilipo lero pakati pa mafuko ndiponso m'chikhaliwe cha anthu sizikanapeza malo. M'kumvera chifuniro cha Mulungu muli mphamvu yakuusintha ndi kupatsa mtendere ku moyo ndiponso kukhalirana mwachikondi pakati pa anthu.

Yesu ali n'kuima pa phiri lina lake m'phepete mwa Nyanja ya Genesereti, analankhula mau akudalitsa ophunzira ake ndiponso khamu linali pa malopo. M'masiku amenewo mzimu wakupembedza moona unali utasokonezedwa ndi miyambo ndi maphunzitsa za umunthu.

"Odala [iwo] ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo; chifukwa adzakhuta." Mateyu 5:6.

Tinene kuti poonjezera mau akuti 'ali akumva njala ndi ludzu' motsindika analakwitsa? Chifukwa chiyani sanangonena, "Odala ali olungama?"

Tithokoze Mulungu, Yesu anatsindika pa mau akuti iwo akumva njala ndi ludzu chifukwa cha chilungamo. Kumva njala ndi ludzu la chilungamo, ndi chinthu chosowa chomwe ambiri tidzichifunitsitsa.

Anachita Yesu'chi chinali cha chilendo, ndipo chasintha kumvetsetsa kwathu za Mulungu ndi chilungamo ndiponso madalitso anaperedwa'wo kwa onse m'khamu'lo. Iye analalitsa anthu omwe ambiri a ife tikanawatemberera.


Molingana ndi Yesu, tiyenera ife kuyandikira ku mpando wa chifumu, modzichepetsa, ndi modzimva kuperewera osati ngati oyera mtima kale.

Ife timaganiza kuti chilungamo ndi m'chitidwe umene ife tiyenera kukhalamo ngati tikufuna kuti tidalitsidwe.

Koma Yesu akuphunzitsa mosiyana. Iye akuti Chilungamo ndi mdalitso; pamene njala ndi chinthu chotiyenereza.

Sitingathe kuchilandira chilungamo cha Yesu kudzera mu ntchito zathu. Ngakhale tikanafunitsitsa chotani kuteru, sikungatheke ife kufikira pa muyeso wokwanira kuchilandira ichi.

Apatu tiyenera kupasamalitsa: Monga m'nthawi ya atomwi anthu anayesetsa kuitenga miyambo ndi ziphunzitsa za umunthu kuti asokoneze nazo chikhulupiriro m'Mau a Mulungu, momwemonso lero, pakunena kuti tiwakonzenso Malemba, kukana chiphunzitsa cha chilengedwe, pakutsatira ziwanda,



pakutsatira nzeru ya umunthu za chimene Mulungu ali, ndikuti chinthu chiri chonse pa chokha chiri mulungu, mdani wa chilungamo akufuna kusokeretsa anthu kuti ayende m'njira zoletsedwa.

Komatu ilipo njira yabwino koposa yomwe ndi: "Koma nzeru yochokera kumwamba iyamba kukhala yoyera, nikhalanso ya mtendere, yaulere, yomvera bwino, yodzala chifundo ndi zipatso zabwino, yopanda tsankhu, yosadzikometsera pamaso. Ndipo chipatso cha chilungamo chifetsedwa mumtendere kwa iwo akuchita mtendere." Yakobo 3:17, 18.

Chilungamo ndi chikhulupiriro zimayendera limodzi: Chilungamo ndiko kuchita moyenera ndi mokhoza, ndipo ndi kudzera mwa ntchito zathu kuti anthu tonse tidzaweruzidwa. Makhaliwe athu amaonetsewa mu ntchito zomwe timachita. Ntchito zimaonetsera ngati chikhulupiriro chathu n'changwiro kapena ai.

Kodi chilungamo n'chofunika bwanji? Chilungamo ndi maziko pomwe pakhazikikapo mpando wachifumu wa Mulungu. Za chilungamo chokhala mwa Yesu kwalembedwa, "Mwakonda chilungamo, ndi kudana nacho choipa. Mwa ichi Mulungu, ndiye Mulungu wanu, wakukudzozeni ndi mafuta a chikondwerero chenicheni koposa anzanu." Ahebr 1:9.

BUKHU LOPATULIKA NDI LOKHALO MAU A MULUNGU

M'Bukhu Lopatulika m'fotokozedwa udindo wonse wa munthu. Solomoni akuti, "Opa Mulungu, musunge malamulo ake; pakuti choyenera anthu onse ndi ichi." [Mlaliki 12:13.] Chifuniro cha Mulungu chionetsedwa m'Mau ake olembedwawa. Palibe munthu adzapeza ponamira za kusapezeka kwake kumwamba ngati sichidzakhalira chifukwa chakuti iye anayalanyaza osafuna kuwamvetsetsa Mau a Mulungu. M'Bukhu Lopatulika choonadi chonse, ndi udindo ndiponso zonse zoyenera kuchita munthu

- Mayankho a zonse'zi alipo, ndipo ndi osabvuta, pali chinthu chimodzi chomwe ndi chofunikira kwambiri: Mtendere ndi Mulungu.
- Munthu angachite bwanji? Angampeze bwanji Mulungu? Tingalandiridwe bwanji ndi Iye? Tingakhale bwanji chifupifupi ndi Iye?

zifikotokozedwa momveka bwino. Udindo wonse ukufotokozedwa m'chifupikitso cha mau a Mpulumutsi. Iye akuti, "Udzimkonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi nzeru zako zonse...Udzimkonda m'zako monga udzimkonda iwe mwini." [Mateyu 22:37, 39.]

Mphatso ya moyo wosatha ikulonjezedwa kudzera m'chipulumutso cha m'chikhulupiriro mwa Khristu. Mphamvu ya Mzimu Woyera imaperekedwa monga cholozera ntchito ya chipulumutso cha munthu. Mphatso ya moyo kwa okhulupirika, ndi chilango kwa anthu ochimwa zifikotokozedwa momveka bwino. Bukhu Lopatulika ndi lodzala ndi chidziwitso cha chipulumutso kwa onse omwe amamvera ndi kuchita ntchito za chikhritsu.

Mtumwi Paulo akuchitira umboni pakunena, "Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitsa, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo; kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino." (2 Timoteo 3:16,17.)

Kukula kwakunyalanyaza malamulo a Mulungu, kwadzetsa kuonjezeka kwa kusokonekera kwa chipembedzo, kuonjezeka kwa kunyada, kukonda zosangalatsa munthu, kusamvera makolo, kudzikonda; zomwe zikupangitsa anthu oganiza mwakuya pena pali ponse kumadzifunsa, 'Chingachitike chiyani pofuna kuthetsa zoipa zogometsa nzeru'zi'? Ndipo yankho la funso 'li likupezeka m'malangizo a Paulo kwa Timoteo, "Lalirika mau." M'Bukhu Lopatulika ndi mokhamo mukupezeka malangizo omwe angathe kuthetsa zoipa'zi. Liri machitidwe a chikhaliwe cha chifuniro cha Mulungu ndiponso chitsimikizo cha luntha la Umulungu. Limatsegula nzeru za munthu kuti athe kumvetsetsa zobvuta zosaneneka za moyo uno, ndipo kwa onse osamala malangizo ake limapatsa chitsogozo changwiro, kuwapulumutsa iwo kuchokera ku njira zosokeretsa zotsogolera kuchionongoke cha moyo.

Awa pokhala mayankho oti palibe munthu anakhoza kumtsutsa Paulo, mtumwiyo anawaonetsera bwino bwino anthu za mwai umene waperekedwa kwa iwo wakukhala amuna ndi akazi omasuka mwa Khristu, amene kudzera mwa chisomo cha mwazi wake wakutsuka machimo ambiri anabvekedwa ndi mwinjira wa chilungamo cha Khristu. M'miyoyo yao munaonetsewa zipatso za Mzimu – "chikondi, kukwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso" (Agalatiya 5:22, 23).

CHILUNGAMO CHAKUCHITIKA MWA CHIKHULUPIRIRO NDI CHIYANI?

M'bale wina amene tiyandikana naye nyumba akuti amawerenga Bukhu Lopatulika tsiku ndi tsiku pofuna kukhala ndi khalidwe ngati la Yesu. Kukhala ngati Yesu kumayenera kuonetsedwa kudzera m'chinthu china chake. Chimenecho ndi "Chilungamo."

Pofuna kuchitanthauzira mwachidule koma mwakuya tingathe kungoti, "chilungamo" ndicho chiyero chakukhala ngati Mulungu. Ndicho kumvera, kuchita ndi kusunga malamulo a Mulungu; monga kwalembedwa, "pakuti malamulo anu onse ndiwo olungama." Masalmo 119:172. Chilungamo cha Mulungu chimaonetsedwa kudzera mwa Khristu. Ife timalandira chilungamo tikamlandira lye. Si mwa ntchito zathu ngakhale zikhale zolimbika bwanji, si pakumpatsa lye mpatso kapena nsembe pomwe timalandira icho; koma chimapatsidwa kwa ulere kwa moyo uli wonse womwe umamva njala ndi ludzu zakuchilandira. Monga thupi limalandira zakudya zolipanga kuti likhale la mphamvu ndi thanzi nthawi zonse, momwemonso mzimu uyenera kukhala pa chiyanjano chosalekeza ndi Khristu. Umulungu umalumikizana ndi umunthu ukakhala kuti mzimu ukumva ludzu lakufuna kukhala ndi Mulungu.

Mau awa ali ndi matanthauzo akuya ndipo ayenera kuwalingirira kufikira kufunika kwa matanthauzowo kutamvetsetsedwa bwino. Chilungamo, chomwenso ndi chiyero, ndipo chiri chiyero chakufanana ndi Mulungu, komwe kuli kuchita mogwirizana ndi malamulo a Mulungu, chimalandiridwa tikamlandira Khristu. Ndipo chimafuna kudziphetsa.

Chikhalidwe cha munthu ndicho chimakhala cholephera mu m'chijanano ichi, koma chikondi cha Mulunguchimamkakamiza lye [Mulunguyo] kuti asaumirize muntho kuchilandira chilungamo chakecho. Koma kuti munthu asankhe mwakufuna kwake kuchilandira ichi. Chiri mpatso yaulere, ngakhale munthu ayenera kutengako mbali kumfunafuna Mulungu, pakumva njala ndi ludzu lakufuna chilungamo chake'cho.

Chilungamo mwa Chikhulupiriro sichiyenera kukhala nkhabakamwa chabe, sichiphunzitsa wamba, koma chiri mphamvu ya moyo yomwenso imausunga moyo ndi kuupatsa chisomo chakuchita mwa ntchito kapena kuti mphamvu yakukhala ngati Khristu.

Chinyengo chachikuru cha anthu anakhalawo m'nthawi ya Khristu chinali

chakuti, munthu wina akangobvomezeza chinthu ngakhale chisakhale kuti ndi chilungamo, anthu onse amatsatira pochitenga kukhala chilungamo. Chikhalirecho, machitidwe a umunthu, ndi kuchita zinthu mwachizolowezi sikokwanira kupulumutsa moyo. Sangadzetze zipatso za chilungamo. Zichitochito zambiri za dziko ndizopitsitsa ndi zodesedwa ndi mbiri za kupha kochitidwa ndi anthu odzikuza achipembedzo. Afaris anadzitenga eni okha kukhala akatakwe a za chipembedzo pa dziko lapansi, koma khalidwe lao lodziona kuti ndi olungama linawapangitsa iwo kumpachika Ambuye wa ulemelero.

Choopta chomwecho chili pakati pathu lero. Anthu ambiri amangodzitcha ndi pakamwa kuti ali akhristu, chifukwa chakuti ali m'zikhulupiriro za mpingo wakutiwakuti. Koma iwo satsatira konse ndi kuchita choonadi m'moyo wao. Samachikhulupirira ndi kuchikonda choonadicho; pakutero akuonetsatu kuti sanalandire mphamvu ndi chisomo zomwe zimadza mwakupatulidwa ndi kuyeretsedwa mwapadera (kudzera m'chikondi cha ngwiro, kumvera kwa ngwiro, ndi kudzikhuthula kotheratu kuchifuniro cha Mulungu) mwa mau a choonadi. Ambiri amanena kuti ali ndi chikhulupiriro cha m'choodadi; koma ngati chikhulupirirocho sichimawapanga kukhala oona mtima, achifundo, ofatsa, opirira, olingirira za kumwamba nthawi zonse, chimawasandukira themberero, ndipo kudzera m'chitsanzo ndi chikoka chao kwa ena, chimakhala themberero ku dziko lapansi.

Chilungamo chimene Khristu anachiphunzitsa ndicho kudzipereka mtima ndi moyo wonse ku bvumbulutsa la chifuniro cha Mulungu. Ochimwa sangathe kukhala olungama pokhapokhapo atakhala ndi chikhulupiriro ndiponso m'chijanano changwiro ndi Mulungu. Umulungu wa m'choonadi amakweza malingaliro ndi kuupanga moyo kukhala wodzipatula.

Ngati timakhulupirira mwa Mulungu, timalimbikitsidwa ndikubvekedwa ndi chilungamo cha Khristu; timalandira ndi kukutidwa ndi mphamvu yake. Zanedwazi Yehova atero, "Kapena mlekeni, agwire mphamvu zanga, nachite nane mtendere; inde, achite nane mtendere." Yesaya 27:5. Tiyenera ife kulankhala ndi Mpulumutsi wathu ngati kuti ali pafupi pambali pa dzanja lathu lamanja. Malingaliro athu akhazikitsidwe pa lye. Tiyanjane ndi kulankhulana naye pakuyenda pa njira, ngakhale pamene tiri m'kugwira ntchito ndi manja athu.

Chilungamo mwa chikhulupiriro

chitanthauza chikhulupiriro chomwe chimafikira ku mpando wachifumu wa Mulungu; ndi kumpanga iye amene ali nacho, "kuona Wosaonekayo." Ahebi 11:27, ndicho kuilandira mphamvu yoperekedwa ndi Mulungu yothandiza pakukula m'khalidwe lomwe ndi lofanana ndi la Yesu. Kukula kwa khalidwe lopambana'lo kudalira pa machitachita osalekeza a chikhulupiriro cha nthawi zonse. Ubale wopambana wachiyanjano cha malingaliro ndi Mulungu uyenera udzilimbikitsidwa. Sitima ya magetsi imapita chitsogolo, ngati mitengo ndi dzingwe za magetsi zokhala pamwamba pake ziri chilumikizirane ndi kugwirabe ntchito zao. Kumva njala ndi ludzu lakuchita chilungamo kuyenera kukhala kukupitirira pakati pa munthu ndi Mulungu ndiponso m'chijanano chosalekeza ndi cholinga chakuti khalidwe lilukike m'makonzedwe a mwinjiro wa chikhazikitso cha kumwamba. Monga momwe moyo umamfunafunira Mulungu, mphamvu yochochera kwa Mulunguyo imapitirira kufalikira m'moyowo kufikira khalidwe litaumbika kukhala la chilungamo ndi lakumva ndi kuchita chifuniro cha lamulo la Mulungu, lomwe ndi muyeso weni weni wa chilungamo.

Chilungamo mwa chikhulupiriro chikufotokozedwanso kuti chiri bafuta wonyezimira woti mbu amene wapangidwa m'makonzedwe akumwamba.

Werengani Chibvumbulutsa 3:4, 5, 18; 16:15; 19:8. Ambuye anagwiritsa ntchito chobvala cha ukwati mu chitsanzo chake chakufunikira kwa kukonzedwa kwa khalidwe, chifukwa mwinjiro unali chinthu chodziwika bwino koto kuti chitsanzo'chi chinali chapafupi kwa anthu kuchimvetsetsa. Ife tonse timadziwa momwe zingwe zolukira nsaru zimapangidwira, ndiponso momwe zingwezo zimalumikizidwira pamodzi kukhala nsaru yomwe imapangidwa mwinjiro. Mu njira iyi Ambuye akutiphunzitsa ife ndi zinthu zomwe timazona, kuzichita pakhomo ndi cholinga chofuna kuchifikira chikumbumtima chathu ndi choonadi cha uzimu kuti makhalidwe athu angathe kupangidwa olungama pokhapokhapo ngati titamayang'ana pa lye tsiku ndi tsiku, ora ndi ora, mphindi ndi mphindi, ndi kuilandira mwa chikhulupiriro mphamvu yomwe lye amaipatsa kosalekeza kwa onse amene amakhulupirira lye. Ndi mu njira ngati imeneyi kuti timalandira chiyenerezo chathu chodzalowa kumwamba. M' mau ena chilungamo ndicho chisindikizo chathu cha kumwamba; ndipo chimatithandiza kupanga khalidwe la

unzika wa kumwambako.

M'Bukhu Lopatulika mwinjiro wa ukwati ukumira khalidwe lomwe anthu onse omwe adzakhale nao pa phwando la ukwati wa Mwanawankhosa ayenera kukhala nalo. M'fanizo la chobvala cha ukwati (Mateyu 22), Ambuye anatsindika kuti pali kukonzekera komwe kuyenera kuchitika ndi onse omwe adzatengeko mbali pa phwando'lo. Onse amene akukunyalaza kukonzekera adzataidwa kunjira. Chilungo cha onse amene akuinyalanyaza ntchito yakukonzekera, yomwe ndi kukula mkhalidwe la chiyero, chikusonyezedwa mwa munthu wopanda "chobvala cha ukwati" uja – yemwe anaturutsidwa ndi kutaidwa kunjira. Chobvala cha ukwati m'fanizo ili chikuimira khalidwe lachiyero, lopanda chirema lomwe onse otsatira oona mtima a Yesu ayenera kukhala nalo.

Mpingo ukuuzidwa kuti wapatsidwa kubvala, 'bafuta wonyezimira woti mbu,' 'wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere.' "Pakuti Bafuta woyera woti mbu," Bukhu Lopatulika likuti, "ndiye zolungama za oyera mtima." Chibvumbulutsa 19:8; Aefeso 5:27). Ali chilungamo cha Khristu, khalidwe lake lopanda banga liri lonse la uchimo, lomwe kudzera mwachikhulupiriro limapatsidwa kwa onse amene amlandira lye kukhala Mpulumutsi wao. ... Chobvala cha ukwati ichi, mwinjiro wa chilungamo wa lye mwini, adzaubveka moyo uli wonse wakulapa ndi kukhulupirira. 'Ndikulungiza,' lye akutero, 'ugule kwa lye ... zobvala zoyera, kuti ukadzibveke, ndi kuti manyazi a usiwa wako asaoneke' (Chibvumbulutsa 3:18). Mwinjiro uwo, wolukidwa m'makonzedwe a kumwamba, siuli ndi mkawo umodzi monga mwamakonzedwe a umunthu.

Tikadzikhuthula ife kwa Khristu, mtima wathu umalumikizana ndi mtima wake, zofuna zathu ndi zofuna zake, malingaliro amakhala amodzi ndi ake, maganizo amakhala pansu pa ulumuliro wa lye; ndipo timakhala moyo wa lye. Ichi ndicho chikutanthauzidwa pakunena kuti kubvekedwa ndi mwinjiro wa chilungamo chake. Koto kuti pamene Ambuye atiyang'ana, samaonanso matewera a masamba a mkuyu, samaonanso umariseche ndi chidetsa cha tchimo, koma mwinjiro wa chilungamo cha lye mwini, womwe, ndi kumvera malamulo a Mulungu kwa ngwiro.

Tiyeni tsono titsegule Mabuku athu Opatulika ndi kuwerenga chomwe chikutanthauzidwa ndi mau akuti chilungamo cha kuchita mwa

chikhulupiriro ndi momwe munthu amachilandirira:

Chikhulupiriro chiri chiyanjano chamoyo ndi Mulungu – dzanja la chikhulupiriro lifikira ku mpando wachifumu wa Mulungu, kumene Yesu, Mkuruwansembe, akutetezera pakati pa Mulungu ndi munthu (1 Timoteo 2:5).

Kumeneko akupempherera kosalekeza onse amene akudza kwa Mulungu mwa lye (Aroma 8:35; Ahebi 7:25).

Kuchokera kumpando wachifumu wa “Ukuru m’Mwamba” – komwe lye anyamula “zonse ndi mau a mphamvu yake” (Ahebi 1:3) kuchokera ku “mpando wachifumu wa Ukuru m’Kumwamba” (Ahebi 8:1), lye amapatsa chifundo ndi mathangato (Ahebi 4:16).

Ndi kudzera mu udindo wake monga Mkuruwansembe kuti lye amapatsa anthu ake mphamvu yakugonjetsa tchimo (1 Akorinto 15:57; Chibvumbulutsa 3:21). Mphamvu imeneyo imatsika kuchokera kwa lye ngati mtsinje wamadzi a moyo ndi kufalikira kwa onse amene moyo wao walunzantsika ndi wake mwa chikhulupiriro. Kulumikizana uku kuyenera kuchitika pakati pa munthu ndi lye chifukwa popanda kutero palibe mphotho idzalandidiridwa.

Pofuna kuonetsera chitsanzo chopambana cha choonadi ichi, Ambuye analowerera ndikuchita chozizwa pakuchitira machiritso mkazi amene “anamwa zowawa zambiri ndi asing’anga ambiri, nalipira zonse anali nazo osachira pang’ono ponse, koma makamaka nthenda yake inakula.” Marko 5:26. Pakumva za zozizwa zomwe Yesu anzichita, mkaziyo anakhulupirira kuti Yesu angathe kumchiritsanso iye. Lye anayesetsa koma sanathe kumuyandikira Ambuye wathu. Koma Yesu amene amadziwa munthu ali yense wokhala pa dziko lapansi, anzindikira kuti mkaziyo anali kufunitsitsa kukomana naye ndi kukhuza mphamvu yake ya machiritso, lye anayandikira ndi kudutsa pafupi ndi mkaziyo. Lye sanangoganiza za momwe angayankhire pemphero la maiyo kokha ; koma anatengerapo mwai wa chochitika’chi kuwatimikizira bwino anthu ake za phunziro lakufunikira kwa kulumikizana ndi lye amene ali Magwero a mphamvu zonse.

Umu ndimo zimafunikira kumachitika m’zinthu za uzimu. Kungolankhula za chipembedo m’mau. Kupemphera popanda kumva njala ya uzimu ndiponso chikhulupiriro cha moyo, sizingapindulitse kanthu. Chikhulupiriro mwa Khristu, chongobvomera m’mau kuti lye ndi

Mpulumutsi wa dziko lapansi, sichingathe kudzetsa machiritso ku moyo. Chikhulupiriro chotsogolera ku chipulumutso sichochitika monga mwa nzeru ya umunthu. Sikokwanira kungokhulupirira za Khristu; tiyenera kungokhulupirira mwa lye. Chikhulupiriro chokhacho chomwe chingatipindulire ife ndi chija chomtenga Khristu kukhala Mpulumutsi wa munthu ali yense payekha, ndipo chimatiyenera ife kulandira mphamvu ya umulungu wake.

Chikhulupiriro chakupulumutsa ndi machitidwe omwe anthu amene amlandira Khristu amadziyanjanitsa iwo eni m’pangano la ubale ndi Mulungu. Chikhulupiriro cha m’choonadi chiri moyo umene. Chikhulupiriro cha moyo ndicho kuonjezeka kwa mphamvu, kudalira mwa Khristu ndiponso kudzera mwa ichi moyo umalandira mphamvu yakugonjetsa.

Kubwerezanso, “chikhulupiriro chakupulumutsa ndicho kukhulupirira Khristu ndi kudziyanjanitsa m’pangano la ubale ndi Mulungu” – sikungolankhula mbiri ya Yesu m’mau kuti anakhalapo moyo pa dziko lapansi ai. Koma kukhala ndi moyo mwa chikhulupiriro chomwe chikutanthauza ora liri lonse ndi mphindi iri yonse – komanso molumikizana kweni kweni ndi Khristu. Mwa ichi zolingirira ziri zonse zimagonja ndi kumvera konse pansu pa ulamuliro wa Khristu. (2 Akorinto 10:5).

“LIMBA NAYO NKHONDO YABWINO YA CHIKHULUPIRIRO, GWIRA MOYO WOSATHA” (1 Timoteo 6:12).

Molingana ndi momwe zimaonekera kulimbana nkondo ndi chikhulupiriro ndi zinthu ziwiri zosatheka kuzilekanitsa. Mau a Mulungu amafotokozza momveka bwino kuti chikhulupiriro popanda kulimbana si chikhulupiriro. Koma iye wakulimbika chilimbikire kufikira chimariziro, yemweyo adzapulumuka. Mateya 24:13. Awa ndi mau athu olowera mphunziro la Nkhondo Ya Chikhristu.

Mtumwi Paulo anamlangiza Timoteo, “ulimbane nayo nkondo yabwino,” “Limba nayo nkondo ya chikhulupiriro,”

“Umve zowawa...monga msilikari wabwino wa Khristu Yesu” (1 Timoteo 1:18; 6:12; 2 Timoteo 2:3). Kawiri konse polankhula za mkhristu monga msilikari wa nkondo, Paulo akuwalimbikitsa anthu, “Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kuchirimika pokana machenjerero a mdierokezi. Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukuru, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a choipa m’zakumwamba. Mwa

ichi mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima chitsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutachita zonse, mudzachirimika.” (Aefeso 6:11-13).

Kenaka mtumwi’yu anafotokozza magawo a zida za Mulungu zomwe ziyenera kubvalidwa ndi wokhulupirira, koma pakunena za chikhulupiriro lye akuti, “koposa zonse mutadzitengeranso chikopa cha chikhulupiriro, chimene mudzakhoza kuzima nacho mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo.” (ndime 14-18). Chikhulupiriro sichimachotsa kulimbana kapena kumenyana, koma chiri chishango chimene chingagwiritsidwe ntchito mwa luntha podzitchinjiriza ku mbi ya mdani – choncho kulankhula kwa Paulo kochiyerekeza chikhulupiriro kuti ndi chishango nkofunikira kwambiri, ndipo kukutimikizira kuti chikhulupiriro ndi kumenyana nkondo ndi zosalekanitsika.

M’lalo mochtenga chikhulupiriro ngati mlowamallo wa kumenyana nkondo, mafotokozedwe a Paulo za mkhristu monga msilikari wa nkondo ndi aja akumonetsera msilikariyo ali mkati mwakulimbana koopsa. Kulimbana kutafika poopsa kwambiri chofunika chinali chikhulupiriro chokha monga chodzitchinjiriza. Pomfotokozza msilikari wa chikhristu mu nkondo yake yolimbana ndikulikonza khalidwe lake kukhala ngati la Khristu, Paulo akumyererekeza iye ndi msilikari wina amene anapita ku dziko limene linali lokanganirana ndi mdani. Paulo akuchenjeza msilikari wa chikhristu kuti adzikhala tcheru kulimbana ndi machenjerero a Satana, chifukwa cholinga cha Satanayo ndicho kufuna kumlanda msilikari’yo dziko lomwe analitenga mobvutikira kukhala lake. Tiyeni timvetsetse mwakuya mau a Paulo, “Mwa ichi mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima chitsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutachita zonse, mudzachirimika kulimbana ndi machenjerero a mdierokezi. Chifukwa kuti kulimbana kwathu tikulimbana ndi Maukuru a za Mdima, akuchita zolimbika a dziko la mdima uno omwe atizungulira ndi a uzimu woipa m’zakumwamba...chirimikani polimbana ndi mdaniyo, kuti mutalimbika kwa nthawi, mukhalebe chilimbikire. Imani nji, osagwedezeka... Muchite ichi mwa pemphero ndi pembezero losalekeza. Pempherani mu mtima mwanu nthawi zonse. Chitani ichi nthawi zonse mosagwedezeka koma ndi chipiriro chonse.” (20th Cent. N.T.).

Mfumu Davide atazindikira kuti maganizo a umunthu ali mdani

wotsutsana ndi Mulungu anamlangiza mwana wake, “Ndipo iwe Solomo mwana wanga, umdziwe Mulungu wa atate wako, umtumikire ndi mtima wangwiro ndi moyo waufulu; pakuti Yehova asanthula mitima yonse, nazindikira zolingirira zonse za m’aganizo; ukamfunafuna lye udzampeza, koma ukamsiya lye adzakusiya kosatha.” (1 Mbiri 28:9).

Satana amalimbikitsa nkondo yake kuwatsekereza anthu kuti asalumikizane ndi Mulungu.

Lye amene watsimikiza mtima kulowa mu ufumu wa kumwamba adzaturukira kuti mphamvu zonse ndi kuipa kwa mtima wokanika, zolimbikitsidwa ndi mphamvu za ufumu wa mdima, zaika kulimbana naye. Choncho tsiku liri lonse ayenera iye kulimbana ndi kumenyana nkondo ya chisalungamo. Zizolowezi zakale, machimo achibadwa otengera kuchokera kwa makolo, adzalimbana naye kuti achite ufumu mwa iye, ndipo pofuna kutsutsana ndi onsewa iye ayenera kulimbika chilimbikire, mu mphamvu ya Khristu yakupatsa chigonjetso.

Nkhondo yakulimbana ndi undekha ndi nkondo yokhayo yoopsa yomwe munthu sanayambe waipewa.

Munthu ali yense amamva mu mtima mwake kulimbana kwakukuru kofunitsitsa kuti akadagonjetsa tchimo. Nthawi zambiri iyi imakhala ntchito yopweteka kwambiri ndi yokhumudwitsa. Koma munthu ali yense amene adzalowe pa zipata za ngale zonyezimira za mzinda wa Mulungu adzayenera kutero pambuyo atagonjetsa, ndipo mdani wamkuru woposa onse ndi woyenera kumgonjetsayo ndi undekha.

“Moyo wonse wa munthu” uyenera kukhuthulidwa kwa Mulungu, ngati tikufunitsitsadi kukhala osinthika ndi kukhala m’fanizo ndi chikhaldwe cha lye. Mwa chikhaldwe ndi chibadwa chathu ndife olekanitsidwa ndi Mulungu, choncho kusiya zonse zoipa ndi kudzanso kwa lye, pafunika kulimbika.

Ntchito iyi (ya kugonjetsa tchimo) ingathe kuchitika mwachipambano pokhapokhapo kudzera mwa chikhulupiriro mwa Khristu, mu mphamvu ya Mulungu. Mkhristu adzakhala akumva dzikakamizo za tchimo m’moyo wake nthawi zonse, chofunika ndi kulimbana nazo zikakamizo’zo kosalekeza. Zikafika pamenepo ndipo timamfunira Khristu kuti atithandize. Zifoko za umunthu zimathetsedwa mu mphamvu ya umulungu, ndipo wokhulupirira amapfuula. “Ayamikike Mulungu, amene atipatsa ife chigonjetso mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” 1 Akorinto 15:57.

manyazi, wolunjika nao bwino mau a choonadi. Koma pewa nkhani zopanda pake; pakuti adzapitirira kutsata chisapembedzo” (2 Timoteo 2:15, 16).

Mau onse a Yesu ali choonadi, ndipo ali ndi matanthauzo akuya ndi ofunikira kuposa m'mene timaganizira tikamangowamva. Yesu anati, “Ndipo mudzazindikira choonadi, ndipo choonadi chidzakumasulani” Yohane 8:32. Monga zimakusokonezani, mukamamva anthu akunena kuti palibe kusiyana kaya wina akupembedza pa Sunday ndi wina akupembedza pa Sabata? Pa magulu awiri'wa lina liri m'chooadi ndi lina m'kusayeruzika, ndipo sabata lina ndi losabvomerezeka ndi Mau a Mulungu. Kutsatira lamulo limodzi lolakwika kumatogolera “kukuchimwira-chimwira.” Nkosatheka kumpembedza Mulungu yemwe ndi Mlenji wosakhala pa tsiku limene lye analipatula kukhala lokumbukira za ntchito yake yakulenga – la Sabata.

Mau onse a Khristu ali ndi matanthauzo kuposa momwe ife timawawerengera. Anthu amene amatogozedwa ndi Mzimu Woyera amamvetsetsa za chiri chonse chomwe Mau'wo amatanthauza.

Chitsanzo cha Petro choyenda pa Nyanja chimaphunzitsa za kufunikira kwa chilungamo chakuchitidwa mwa chikhulupiriro, komanso kupindula kosaneneka komwe timakupeza tikamayang'ana pa Yesu. Nthawi yonse imene Petro anayang'ana kwa Yesu, anayenda pamwamba pa madzi (Mateyu 14:25-31). Koma anamira pamene analeka kuyang'ana pa Mpulumutsiyo.

Mphamvu yodabwitsa imapatsidwa kwa iwo amene amamvetsetsa chiphunzitsa chopatsa moyo ichi – “Ndikupenyereka [Yesu] woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiriro chathu... Ndi kuyang'anira pasakhale wina” (Ahebri 12:2, 15). Chigonjetso chalonzjedwa kwa onse amene amayang'ana kosalekeza pa Yesu, lye amene ali chiyambi chamayendedwe a chikhristu chathu – yemwe ngati ife titapitiriza kuyang'ana pa lye, adzatsirizadi ntchito imene anaiyamba mwa ife. Chofunika ndi kungoyang'ana pa lye kosalekeza.

Cholinga cha Satana ndicho kufuna kuwasokoneza anthu kuti asiye kudalira kwatunthu pa tchinjirizo la chikhulupiriro chao, kuti asiye kuyang'ana kumwamba pa Yesu. Onse amene amayang'ana pa Yesu kosalekeza amalandira mphamvu yake, iwo amene amasiya kuyang'ana pa lye amaphimbidwa ndi mdima umene umakhala kwa iwo uli chofunda wochokera kwa angelo akugwa. Choncho kulimbana kwakukuru kwa m'masiku otsiriza ano kuli makamaka

nkhondo ya mphamvu za Satana zomwe zikuyesetsa kuwatchinga anthu a Mulungu kuti asamayang'ane kwa Yesu ndi cholinga chakuti alekanitsidwe ndi mphamvu ya chigonjetso chao.

Choonadi chachkuru chatsindikizidwa ndi alembi a Chipangano Chatsopano – chakufotokoza za kufunikira kwa kuyang'ana pa Yesu mu utumiki wa ukuru-wa-unsembe wake pa dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Atate wake. Paulo akuti: “Funani za kumwamba kumene kuli Khristu wokhala pa dzanja lamanja la Mulungu. Lingirirani [ganizani mwakuya] zakumwamba (Akolose 3:1,2). Iye anawalangiza Ahebri anabwerera m'mbuyo'wo pa chikhulupiriro chao (4:16), kuyandikiranso ku “mpando wachifumu wachisomo,” chifukwa kumeneko “tiri naye Mkurowansembe wamkuru, Yesu Mwana wa Mulungu.” Kumeneko, kwakhazikikako chiyembekezo chathu: “Chimene tiri nacho ngati nangula wa moyo, chokhazikika ndi cholimbanso, ndi chakulowa m'kati mwa chopimba; m'mene Yesu mtsogoleri wathu analowamo chifukwa cha ife, atakhala mkuru wa ansembe nthawi yosatha monga mwa dongosolo la Melikizedeke.” “Kuchokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa lye, popeza ali nao moyo wake chikhaliye wa kuwapembedzera iwo.” “Ndipo popeza tiri naye wansembe wamkuru wosunga nyumba ya Mulungu; tiyandikire ndi mitima woona... Ndi kupenyereka [mwa Yesu] Woyambirira ndi Womariza wa chikhulupiriro chathu” (Ahebri 4:13-16; 6:19, 20; 7:25; 10:19-22; 12:2). Paulo m'kalata wake wa ku Aefeso akufotokozanso momveka bwino zamadalitso ochuruka omwe akudikira okhulupirira mwa Khristu, onse amene akuyang'anitsa kwa lye amene anakwezidwa ku Mpando Wachifumu wa Chisomo kukhala Nkhoswe ya anthu, komwe Atate anamkhakizitsa “pa dzanja lake la manja m'zakumwamba, pamwamba pa ukuru wonse, ndi maulumuliro, ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lotchedwa” (Aefeso 1:19-22; 3:10-21). Mtumwi Petro wosakhazikika maganizoyoy, amene anasinthidwa kuchokera pakukhala wofoka kupita kukhala wochirimika, akumfotokozanso Yesu Khristu kuti ali, “amene anakhala pa dzanja lamanja la Mulungu atalowa m'Mwamba; pali angelo, ndi maulumuliro, ndi zimphamvu, zomgonjera” (1 Petro 3:22).

Kudzera mwa moyo ndi imfa yake, Khristu wachita zazikuru zoposa populumutsa miyoyo yomwe inataika


chifukwa cha tchimo. Chinali cholinga cha Satana kudzetsa kulekana kwa muyaya pakati pa Mulungu ndi munthu; koma mwa Khristu tikulunzanitsidwa ndi kuyandikitsidwa pafupi kwambiri ndi Mulungu koposa kale ngati kuti sitinachimwepo konse. Pakutenga umunthu wathu, Mpulumutsi anadzilumikiza Mwini Yekha ndi mtundu wa anthu mu ubale umene sungathe kuswekanso. Ku zaka za muyaya ayanjanitsidwa lye ndi ife. “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi koto, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira lye asataike, koma akhale nao moyo wosatha” Yohane 3:16. Atate sanampereka Mwana wake kudzangosenza machimo athu ndi kudzatifera kokha, anapatsa lye ku mtundu wakugwa wa anthu. Pofuna kutitsimikizira uphungu wake wosatha wa mtendere, Mulungu anapatsa Mwana wake wobadwa yekhayo kukhala m'modzi ndi banja la umunthu, kuti akhale m'maonekedwe ngati munthu kwa muyaya. Ukutu ndi kukwaniritsa kwa Mau a Mulungu akuti, “Pakuti kwa ife mwana wakhandu wabadwa, kwa ife, mwana wamwamuna wapatsidwa; ndipo ulumuliro udzakhala pa phewa lake.”

Yesu ndipo lye yekhayo ndiye Nkhoswe ya pakati pa Mulungu ndi mtundu wonse wa anthu, amene agwirizanso mbali ziwirizi. Iye amene ali “woyera mtima, wopanda choipa, wosadetsedwa, wosiyana ndi wochimwa, wakukhala wopitirira miyamba,” sachita manyazi konse kutitcha ife abale ake. Ahebri 7:26; 2:11. Mwa Khristu banja la dziko lapansi ndi banja lakumwamba amangika pamodzi. Khristu wokwezidwaye ali m'bale wathu. Kumwamba kuonekera mu umunthu, ndipo umunthu ukhalitsa muyaya m'chifungatiro cha chikondi chosaneneka cha Atate.

Tisaiwale kuti Khristu analandira chilango chotiyenera ife, kuti ife tikonedwe ndi Atate monga lye. Iye anazunzidwa chifukwa cha machimo amene sanatengeko mbali kuwachita, kuti ife tiyeretsedwe mwachilungamo chake chomwe ife sitinatengeko mbali kuchikhazikitsa. Iye anamva zowawa za imfa yomwe inali yathu, kuti ife tilandire moyo umene uli wake.

Gologotha akutsimikizira chipamabano cha ntchito yake yakupulumutsa. Ndipo ndi udindo wa munthu kuchilandira chikondi chachikuruchi, chifukwa ndi chipulumutso choposa choterechi, chisomo cha Ambuye chachipanga ichi kukhala chotheke kuti munthu alandire moyo. Tiyenera ife kuonetsa kuthokoza

kwathu za mpatso ya mtengo wapatali ya Mulunguyi potipanga kukhala wogawana naye umulungu wake, titapulumsidwa kuchoka kuchibvundi cha za m'dziko lapansi zomwe zimadza chifukwa cha chilakolako. Tikuyenera ife kuonetsa kuyamika kwathu kwa Mulungu pakukhala ife ogwira ntchito limodzi ndi Yesu Khristu, polionetsera khalidwe lake ku dziko lapansi. Ambuye amationa ife monga ngale za mtengo wapatali.



ZA YESU

Yesu akuti, “Taanani, ndakupatsani ulumuliro...pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo” Luka 10:19, - osati pa zocheperapo za “mphamvu za mdaniyo” koma “pa mphamvu iri yonse ya mdaniyo.” Ichi ndi chomwe Mau a Mulungu akutanthauza pakunena za iwo amene adalira pa lye, “m'zonsezi, ife tilakatu” (Aroma 8:37). “Ayamikike Mulungu amene atipatsa ife chigonjetso mwa Ambuye wathu Yesu Khristu” (1 Akorinto 15:57; 2 Akorinto 2:14). “Pakuti chiri chonse chakubadwa mwa Mulungu chililaka dziko lapansi; ndipo ichi ndi chilako tililaka nacho dziko lapansi, ndicho chikhulupiriro chathu;” “ndipo inu mwawalaka iwo (aphunzitsi onyenga),” “ndipo mwamla m'daniyo.” (1 Yohane 5:4; 4:4; 2:14).

Onse amene amapereka kwa Mulungu matupi, moyo ndi mitima yao, amalandira mphamvu yatsopano kosalekeza ku moyo wao wa thupi, maganizo ndi wa uzimu. Akasupe osaphwa komwe kumachokera mphamvuzo amakhala okonzeka kuwathandiza nthawi zonse.

“Uthenga Wabwino wa Khristu...uli mphamvu ya Mulungu ya kupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira” Aroma 1:16. Iyi imaonetsedwa m'machitidwe “akubadwanso” omwe amatheka mu

mphamvu ya Mzimu Woyera yokha. Uthenga Wabwino sumangokhala njira imene mphamvu yimadzera koma kuti uli mphamvu ya Mulungu yomwe imagwiranso ntchito yakupulumutsa onse amene akhulupirira. Mphamvu ya Mulungu'yi simangokhuzidwa ndi chipulumutso cha wokhulupirira m'modzi m'machitidwe ake, koma imamlimbikitsanso wokhulupirirayo kulalikira kwa ena. Ambuye Yesu anati, "Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine...Chifukwa chake mukani." (Mateyu 28:18, 19). M'mau awa lye akuonetsa kuti akuigwiritsa mphamvu ya Umulungu wakeyi pa udindo wake wakukhala mutu wa mpingo. Akulimbikitsa omtsaira ake panso pano kupita pa dziko lapansi lonse ndi kulalikira uthenga wabwino podalira pa mphamvu yake yoposayi. Ogwira ntchito a Mulungu samakhala odzimwa mwa umunthu akakhala akudalira kotheratu pa Ambuye kukwaniritsa malonjezanso ake oposa pakugwiritsidwe ntchito mphamvu ya Umulungu wake.

Chitsimikizo chakuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu, Mwini chilengedwe chonse ndiponso Wokhala ndi machitidwe onse a mphamvu ya Mulungu, ndicho maziko a mpingo wa chikhristu – Werengani Mateyu 16:16-18; 1 Akorinto 3:11; 1 Petro 2:5-8. Chifukwa chiyani nanga Chipangano Chatsopano chikulankhula motsindikira kwambiri kuti Yesu sanali mulungu wamba koma Mlengi wa zinthu zonse? Chifukwa choonadi ichi ndi chofunikira kwambiri ku chipulumutso chathu. Maganizo obwerera m'mbuyo omwe anthu ambiri ali nao onyozetsa khalidwe la Umulungu ndi ntchito ya Khristu zapangitsa anthu'wo kukhala ndi machitidwe ofoka m'chipembedzedwa chao, ndi kutsekereza ndiponso kuulowetsa panso moyo wao wa uzimu. Iye, kodi tikufuna titazindikira mwakuya za Umulungu wa Ambuye kapena za machitidwe ake ena oonetsa za Ukuru wake ndi za mphamvu zake zotsimikizira kuti ali Mkuruwansembe amene ali pa mpando wachifumu wa Atate? "Koma mutu wa izi tanenazi ndi uyu. Tiri naye Mkuruwansembe wotere, amene anakhala pa dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Ukuru m'Kumwamba, Mtumiki wa malo opatulika, ndi wa chihema choona, chimene Ambuye anachimanga, si munthu ai" (Ahebri 8:1, 2).

"Mkuruwansembe" uyu (Ahebri 4:14) ndi wofana m'zonse ndi Atate wake. "...Khristu Yesu: Ameneyo, pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu" (Afilipi 2:6). "Mulungu... Mwana... Ameneyo, pokhala ali m'chiyeretso cha ulemelero

wake, ndi chizindikilo cheni cheni cha chikhaldwe chake, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yake, m'mene adachita chiyeretso cha zoipa, anakhala pa dzanja la manja la Ukuru m'Kumwamba" (Ahebri 1:1-3).

Mtumwi Paulo anasankhidwa mwapadera kukhala mtumiki wofotokoza momveka bwino za ziphunzitsa za choonadi zomwe zinali zofunikira kwambiri kuti anthu amtundu wake azimvetsetse. Tatiyeni tiwerenge ndi kuona momwe Paulo analankhulira mwakuya komanso kwa nthawi yaitali kwambiri za kufunikira kwa kumvetsetsa za ulemelero ndi kukhala Mulungu wopanda chiyambi kwa Khristu; tiyeni tiyang'anitsitse kufanana kwa kafotokozedwe kwa dzina la Khristu komanso la Mulungu Atate ndi la Mulungu Mzimu Woyera, pomwe mtumwiyo akufotokoza kuti, "Pakuti mwa lye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yachifumu, kapena maufumu, kapena maukulu; zinthu zonse zinalengedwa mwa lye ndi kwa lye. Ndipo lye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa lye. Ndipo lye ali mutu wa thupi, Eklesiyayo... Pakuti kunamkomera Atate kuti mwa lye chidzalo chonse chikhali" (Akolose 1:16-19). M'kalata yemweyonso, mtumwiyo akunena, "Pakuti mwa lye chikhali chidzalo cha Umulungu m'thupi, ndipo muli odzazidwa mwa lye, ndiye mutu wa ukulu wonse ndi ulumuliro" (Akolose 2:9, 10).

"Ndipo adzamutcha dzina lake Emmanuel; ndilo losandulika, Mulungu nafe" Mateyu 1:23). "Iye (Mulungu)... anaonekera m'thupi" (1 Timoteo 3:16). "Namwa onse [Aisrayeli akalewo] chakumwa cha uzimu chimodzimodzi; pakuti anamwa mwa thanthwe lauzimu lakwatsata; koma thanthwelo ndiye Khristu. Koma ochuruka a iwo Mulungu sanakondwera nao" (1 Akorinto 10:4, 5). M'mau awa Paulo akufotokoza momveka bwino kuti Mulungu wa Mkurukuru amene anaturutsa Aisrayeli mu ukapolo wa Aigupto ndi kuwatsogolera m'chipululu pa ulendo wao wopita ku Kanani, Mulungu mwini mphamvu zonse yemwe anachita zozizwa kwa Aisrayeli, sanali wina koma "Khristu." Anali Yesu asanabadwe m'thupi la umunthu amene anayenda nao. Pogwiritsa ntchito choonadi chodabwitsa chinachitika kalechi, mtumwi wodzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu'yu akufotokoza za ulendo wa akhristu wopita ku Kanani wa Kumwamba, kuti Mulungu yemwe ndi "Khristu" Mpulumutsi adzapitiriza kuyenda nao.

"Koma izi zinachitika kwa iwowa monga zotichenjeza, ndipo zinalembedwa kutichenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya panso pano adafika pa ife.

"Chifukwa chake iye wakuyesa kuti ali chiriri, ayang'anire kuti agagwe.

"Sichinakugwereni inu chiyeso koma cha umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mukhoze kupirirako [ichi]" (1 Akorinto 10:11-13). Lonjezanso lolimbikitsa bwanji kwa ife, okhala nthawi ya kumapeto a dziko'fe!

Pa nthawi ya utumiki wake wa pa dziko lapansi Ambuye wathu anadzifotokoza kuti ali Mulungu. Iye anachita ndi ulumuliro wonse zomwe Mulungu akanachita, mwachitsanzo kukhululukira machimo (Marko 2:5-11; Luka 7:48-50). Ayuda anakhoza pakunena za lye, "Akhoza ndani kukhululukira machimo, koma mmodzi, ndiye Mulungu?" Mau awa anawalankhula iwo chifukwa Yesu ali m'thupi la umunthu, anamuza mkazi Msamariya motsindikira pa chitsime paja kuti lye anali Mwana wa Mulungu ndiponso Mpulumutsi wolonjezedwayo (Yohane 4:25, 26). Yesu anafotokozanso kuti ali ndi mphamvu ya kupatsa moyo wosatha kwa anthu onse amene lye, mu chikhazikitso cha Umulungu wake angawaone kukhala oyenera kuilandira m'phatso ya ulereyo. "Mwana apatsa moyo iwo amene lye afuna. Pakuti Atate saweruzi munthu ali yense, koma anapereka kuweruzi konse kwa Mwana; kuti onse akalemekeze Mwana, monga alemekeze Atate" (Yohane 5:21-23). Iye anaonetsera poyera kuti ali ndi mphamvu pa chilengedwe chonse, ndi kutinso ali ndi mphamvu yakulenga – Werengani Luka 9:16, 17; Yohane 2:9, 10; Marko 2:5-12.

Yesu anakulandira kupembedza komwe kumayenera kuchitidwa kwa Mulungu yekha. N'chifukwa poyesedwa ndi Satana anamyankha, "Choka Satana pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzangwadira, ndipo lye yekha udzamlambira" (Mateyu 4:9, 10). Yesu anakulandira kupembedzedwa kuli konse kumene kunamchitikira lye – Werengani Mateyu 14:33; Yohane 9:35-38; Mateyu 28:9. Pambuyo pa chozizwa cha kugwira nsomba zochuruka Petro "anagwa panso pa maondo ake a Yesu nenena, Muchoke kwa ine, Ambuye chifukwa ndine munthu wochimwa" (Luka 5:8). Petro anaona chiyero ndi mphamvu ya Umulungu. Mwa Yesu anaonamo lye amene agwiriziza chilengedwe chonse panso pa ulumuliro

wake. Ukuru ndi chiyero cha Umulungu zinadzudzula chisalungamo cha Petro.

Ambuye wathu anadzifotokoza kuti ali wofanana mphamvu ndi Mulungu Atate, komanso wofanana Naye m'chikhaldwe. Iye nati anachita ntchito yofanana ndi yomwe Atate amachita (Yohane 5:17); anali m'modzi ndi Mulungu (ndime 18 ndiponso Afilipi 2:6); anagwiritsa ntchito mphamvu yofanana ndi ya Atate (Yohane 5:21); ndipo analandira ulemu monga Atate (v.23). Anadzifotokoza kuti ali "INE NDINE," Mulungu Wamkurukuru amene anapulumutsa Aisrayeli ku ukapolo wa Aigupto (Yohane 8:51-59). Iye akudzifotokozanso kuti ali "Kuunika kwa dziko lapansi" (Yohane 8:12; 9:5), ndiponso mmodzi ndi Atate (yohane 10:30). Iye sanatsutse Ayuda pamene anamuza, "Chifukwa cha ntchito yabwino sitikuponyani miyala, koma chifukwa cha mwano... muli munthu, mudziyesa nokha Mulungu." Ndipo lye anawayankha iwo, "Kodi inu munena za lye, amene Atate anampatula namtuma ku dziko lapansi, Uchita mwano; chifukwa ndinati Ndiri Mwana wa Mulungu? Ngati ndichita ntchito za Atate... khulupirani ntchitozo kuti mukadziwe ndi kuzindikira kuti Atate ali mwa Ine, ndipo Ine ndiri mwa Atate" (Yohane 10:31-38). Iye anadzifotokoza kuti ali woweruzi wa anthu onse (Yohane 5:26, 27); ndi kuti pa tsiku la chiweruzo chotsiriza mafuko onse adzasonkhana patsogolo pa mpando wake wachifumu (Mateyu 25:31-36); ndipo iwo adzaweruzidwa ndi mau amene lye analankhula (Yohane 12:48); kutinso kuukitsidwa kwa akufa kudalira pa lye (Yohane 6:39, 40). M'bukhu la Chibvumbulutso lye akuti, "Ndine... Ambuye... Wamphamvuyonse". Yerekezani ndi Chibvumbulutso 22:13, 16.

Kunena mwatchutchutchu chiri chonse cha Yesu cholembedwa m'Chipangano Chatsopano chikuchitira umboni za Umulungu wake – kuphatikiza mafotokozedwe, malangizo ndi chiphunzitsa chiri chonse. Chiphunzitsa cha Bukhu Lopatulika za chilengedwe, chipulumutso, utumiki wa kumwamba, chiweruzo, kubwera kwachiwiri, mdzukuro wa akufa, moyo wosatha, kwao kwa opulumutsidwa, chionongoke cha osalungama, utumiki wa Mzimu Woyera, angelo, mpingo – zonsezi nzosalekanitsika ndi mphamvu yonse komanso nzeru ndi luntha za Umulungu wa Ambuye Yesu. Zonse zimene zalembedwa m'Bukhu Lopatulika zikulalikira ndi liu limodzi lalikuru kuti Yesu ndi Mulungu ndiponso kuti maulosi ndi makwaniridwe a chiyembekezo ndiponso malonjezanso

zikhazikika pa machitidwe a mphamvu ndiponso luntha lake lofikira ponse ponse. Posachedwapa kumwamba kutseguka ndipo kuchokera komweko lye adzaonekera alikutsika pamwamba pa khamu lalikuru la angelo osawerengeka. "Ali nalo pa chobvala chake ndi pa nchafu yake dzina lolembedwa, MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE" (Chibvumbulutso 19:11-16). Pamenepo mpfuu ya liu lake lalikuru idzamveka padziko lonse lapansi, ndipo oyera mtima osawerengeka anagonawo mpfumbi lapansi adzauka kukomana naye mumlengalenga (1 Atesalonika 4:16-18; Yohane 5:28, 29).

Mau amene Paulo anawakondetsa pakunena za Yesu ndi akuti, "Mpulumutsi wathu Mulungu (Tito 2:10, 13; 3:4, 6).

Ganizo liri lonse, liu, ndi ntchito zimakhala pamaso ndi pansu pa chisamaliro chosalekeza cha Ambuye Yesu. "Amene akhoza kuthandiza iwo amene ayasedwa" (Ahebi 2:18), chifukwa pokhala munga munthu, lye amadziwa bwino za chifoko cha munthu kuti chimadalira pa mphamvu ya Umulungu, ndiponso, kuti pokhala lye Mulungu, ali nayo mphamvu yoposa yomwe angathe kuigwiritsa ntchito kuthandizira onse amene aitanira pa lye kuti awapululumutse. "Kuchokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa lye, popeza ali nao moyo wake chikhalire wakuwapembedzera iwo" (Ahebi 7:25).

Chikhulupiriro mu Umulungu wa Khristu ndi chofunika ku chipulumutso. Umulungu wa Khristu uli maziko a moyo wosatha. Chilungamo chakuchita mwa chikhulupiriro chiri ndi maziko ake otambalala ndi olimba pa chiphunzitsa cha Umulungu wa Khristu chifukwa chilungamo chimalandiridwa mwa chikhulupiriro kudzera mu mphamvu yosalekeza yochokera ku Kasupe wosaphwa wamoyo. Mphamvu yofunikira kuti munthu akule m'chilungamo imachokera kwa Khristu Yesu mu ntchito yake yakutetezera anthu onse amene amadza kwa Mulungu kudzera mu utumiki wa unsembe wake.

Ndi Mulungu wamphamvu yonse yekhaya amene angathe kukwaniritsa zofuna za munthu, kuyankha mapemphero ake osawerengeka ndi zifunsiro komanso zosowa zake zonse. Zowawa zosaneneka zobwera chifukwa cha uchimo, machenjerero osawerengeka a woipayo ndi myandamyanda ya machitidwe ake a chipongwe, kudzanso chifooko cha munthu, zonse zikumathetsedwa mwa

luso ndi mphamvu yaikuru ya Mulungu. Ndi Mpulumutsi wokhala ndi mphamvu ya Mulungu yekhaya yemwe angathe kukwaniritsa zokhumba za munthu kuyambira za moyo uno mpaka za moyo wa mtsogolo.

Kuti Umulungu wa Khristu ndi wofunikira ku chipulumutso zikutsimikizika ngati tingamvetsetse mau omwe Ambuye anawalankhula'wa, "Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi...ngati simukhulupirira kuti INE NDINE [liu "lye" mulibe m'Chihelene, munga zikuonetsedwa ndi tidzilembo towonderato), mudzafa m'machimo anu" (Yohane 8:12, 24). Poyamba mau'wa angakhale opanda tanthauzo ndi osamveka konse, koma kuwalingirira mwakuya tingathe kuturukira kuti Ambuye amalankhula maziko a choonadi cheni cheni, chifukwadi chipulumutso chidalira pa mphamvu ya utumiki wa Khristu pa iwo amene amadza kwa Mulungu mwa lye. Palibe Magwero ena komwe kungachokere mphamvu - Khristu ndi lye yekhaya amene amapatsa mphamvu zonse zomwe anthu amapulumsidwa nazo. Mphamvuzo sizinali zolengera chilengedwe kokha komanso zogwiriziza miyamba.

Kuti miyamba ikhale m'malo mwao kumafunikanso mphamvu zakuyigwiriziza munga zinafunikira pakulenga zinthu zonse. Choonadi chopambana'chi chikuchitiridwa umboni ndi Bukhu Lopatulika momwe olemba odzadzidwa ndi Mzimu akale anaphunzitsanso za nzeru ya chipulumutso. Ichi ndi choonadi chomwe Paulo anachilalikiranso pakufuzana kumveketsa bwino za ntchito yokhuzana ndi unsembe wa Khristu. lye anati, "Mulungu...masiku ano...analankhula ndi ife mwa Mwana wake...mwa lyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe; ameneyo, pokhala ali chinyezimiro cha ulemelero wake, ndi chizindikilo cheni cheni cha chikhalidwe chake, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yake, m'mene adachita chiyeretso cha zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukuru m'Mwamba" (Ahebi 1:1-3).

Yesu analenga maiko onse; koma zinthu ziri choncho, kuposera apo, akupitirizabe kugwiriziza "zonse ndi mau a mphamvu yake;" komanso kupitirizanso apo, lye akupitirizabe kupatsa mphamvu yakuwasunga anthu amene akumfunafuna lye kuti apulumutsidwe. Maiko akusungidwa m'chilengedwe chao, akuyenda m'njira zao osagwa pomvera mau ndi maweruzo a Mwana wa Mulungu. lyenso amawagwiriziza kosalekeza. Mu mchitidwe womwewo lye amagwiritsa

ntchito chidziwitso ndi Ukuru wa mphamvu za Umulungu wake wopanda malire pogwiriziza anthu ake onse okhulupirira. "Ndipo kwa lye amene akhoza kukudikirani mungakhumudwe, ndi kukuimikani pamaso pa ulemelero wake opanda chirema m'kukondwera, kwa Mulungu yekha, Mpulumutsi wathu, mwa Yesu Khristu Ambuye wathu, zikhale ulemelero, ukuru, mphamvu, ndi ulamuliro zisanayambe nthawi, ndi tsopano, ndi kufikira nthawi zonse." Amen" (Yuda 24, 25).

"Pakuti mwa lye zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yachifumu, kapena maufumu, kapena maukuru, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa lye ndi kwa lye. Ndipo lye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa lye. Ndipo iye ali mutu wa thupi, Mpingo'wo...Pakuti kunamkomera Atate kuti mwa lye chidzalo chonse chikhalire" (Akolose 1:16-19). Tatiyeni timvenso za chifukwa chimene chilengedwe kapena ife tikukhalakobe m'thawi ino - "zinthu zonse zinalengedwa mwa lye, ndi kwa lye." M'mau ena ife ndife ake a Mulungu. M'mau ena ochokera m'Bukhu Lopatulika, tikuzidwa, "Pakuti munagulidwa ndi untendo wake wapatali; chifukwa chake lemekezani Mulungu m'thupi lanu" (1 Akorinto 6:20). Mtengo wake wapatali'wo ndi chiyani? - Mwazi wantengo wapatali wa Yesu.

Kuonjezera apo ntchito ya Khristu munga Mpulumutsi wa Mpingo ikutchulidwa mokhuzana ndi choonadi chakuti lye sanangokhala Mlengi wa zinthu zonse kokha, koma "mwa lye zinthu zonse zigwirizana pamodzi" kapenanso kuti zikhala chikhalire mwamak hazikitsidwe a chilengedwe chao. Zoonadi mphamvu yomwe ija yomwe imagwiriziza miyamba mphindi ndi mphindi ndi yomwenso ikugwiritsidwa ntchito kumsunga munthu m'mayendedwe a moyo wake wa uzimu mphindi ndi mphindi.

Choncho ndi kofunikira kwambiri kuti wokhulupirira ali yense adziwamvetsetsa Umulungu wa Yesu, kuti lye ali Mlengi wa moyo uli wonse ndi maiko onse ndi kuti akugwiritsa mphamvu ya ukuru wake wosayerekezekayi m'ntchito yake yakupulumutsa mtundu wa anthu. Choonadi ichi chikufotokozedwa mobwerezabwerezera ndi motsindika m'Bukhu Lopatulika kuti Mlengiyo alinso Mpulumutsi yemweyo, ndipo mu ndime zomwe choonadi ichi chafotokozedwa pali kutsindika kwapadera pa mfundo yakuti mphamvu yake yakupulumutsa ikuchitika chifukwa lye, pokhala Mlengi, ali ndi mphamvu yoposa yotha kuchitiranso chiombolo - werengani

Yesaya 43:1-3, 11-14; 44:6, 24; 45:11-13, 17, 18; Yohane 1:1-3, 12-14; Akolose 1:14-20; Ahebi 1:1-3.

M'bukhu la Yesaya kuyambira ndi mau akuti, "Mutonthoze, mutonthoze mtima wa anthu anga, ati Mulungu wanu," (Yesaya 40:1), Mulungu akudzibvumbula Mwini Yekha munga Mlengi ndi Mpulumutsi wa anthu ake. Palibenso malo ena ali onse m'Bukhu Lopatulika lonse pomwe pakupezeka chitsimikizo chonenedwa mobwerezera bwereza za mfundo yakuti Mulungu ali yemweyo Mlengi ndi Mpulumutsi wa Israyeli. Pofuna kuwatsimikizira anthu ake kuti lye akugwiritsa ntchito mphamvu ya ukuru wake kuwatchinjiriza iwo ku tchimo, ndiponso kuchokera kwa adani ao, lye akuchifotokoziza ichi pouwonetsera ukuru wake kuti ali Mlengi wa zinthu zonse. Tsono pouyerekeza ukuru wa mphamvu zakezo dziko lapansi ndi zonse ziri momwemo sizinga kanthu konse (Yesaya 40:12-25). Timvetsera za kubetchera kwake, "Kwezani maso anu kumwamba, muone amene analenga izo, amene aturutsa khamu lao ndi kuziwerenga; azitcha zonse maina ao, ndi mphamvu zake zazikuru, ndi popeza ali wolimba mphamvu palibe imodzi isoweka" (Ndime 26).

Kenaka tiyeni timvetsera momwe akukugwiritsira ntchito kubetcherako podzifotokoziza lye mwini munga Mlengi amene amadziwa maina a miyandamiyanda ya madzuwa ndi maiko ndiponso lye munga wosamalira wa zonse, "ndi mphamvu zake zazikuru," lye akuti, "Koma tsopano atero Yehova, amene analenga iwe...ndakuombola iwe, ndakutchula dzina lako, iwe uli wanga" (Yesaya 43:1). Choonadi ichi chakuti Yesu munga Mlengi amadziwa maina a anthu onse a pa dziko lapansi chikutsimikizikanso pamene Yehova analankhula za Koresi, mfumu ya Aperezi, "...kuti udziwe kuti Ine ndine Yehova, amene ndikuitana iwe dzina lako, ndine Mulungu wa Israyeli. Ndakuitana iwe dzina lako, chifukwa cha Yakobo mtumiki wanga ndi Israyeli wosankhidwa wanga; ndakuonjezera, ngakhale iwe sunandiziwa Ine" (Yesaya 45:3, 4).

Apatu Yehova akutionetsera mosakaika konse kuti akugwiritsa ntchito mphamvu yaukuru wake yomweyo pakuitana ndi kusamalira anthu oyera mtima munga momwe amachitira pakuitana ndi kugwiriziza zolengedwa zonse zosawerengeka kuphatikiza khamu la nyenyezi za kumwamba munga mwamakulidwe ao. Masamalidwe a zonsezo akuchitidwa ndi mphamvu yosayerekezekeza ya Munthu m'modzi yemweyo, Mlengi -

Mpulumutsi wathu.

KUYANG'ANITSITSA PA YESU

Ambuye wathu akutiya kuti tidzalandira m'phamvu ngati tiyang'anitsitsa kwa Iye. (Yesaya 45:22). Tikadalira ndi kuyang'anitsitsa kwa Iye kosalekeza m'phamvu yathu idzakhalayaukuuri ndi yochuruka. Munthu sangachimvetsetse chinthu ichi.

Pemphero losalekeza liri kulumikizana kwa uzimu wangwiwo ndi Mulungu, ndiponso njira yomwe m'phamvu yamoyo wochokera kwa Mulungu imafikira m'moyo wathu.

Timayang'ana kwa Mulungu kudzera m'pemphero – kutanthauza pamene tapemphera moyenera. Kuti pemphero likhale lomveka liyenera kuperekedwa kwa Mulungu. Maganizo ndi moyo wathu wonse ziyenera kukhazikika pa Iye. Tiyenera kutengera phunziro monga anachitira Mose, amene pochitira umboni za Iye Bukhu Lopatulika likuti, “pakuti anapirira molimbika, monga ngati kuona wosaonekayo” (Ahebrei 11:27).

Apatu chikuperekedwa chinsinsi cha m'phamvu, chinsinsi cha chipambano, chinsinsi chakulimbika chilimbikire – kukhazikitsa moyo wonse pa Iye Wosaonekayo. Kuika maganizo onse kwa Mulungu pamene m'phamvu ikulowa m'moyo wathu.

Tiyang'anitsitsa kwa Yesu. Maganizo onse akhale pa Iye, alingilire mwakuya za chikondi chake, ubwino wake, ndi ungwiro wa khalidwe lake. Maganizo akangokhazikika pa undine, ndiye kuti sakulumikizananso ndi Khristu, yemwe ndi magwero a chilimbiko ndi a moyo. Ichi ndicho chimakhala cholinga cha Satana nthawi zonse, kukhotetsa chidwi chathu pakuchichotsa kwa Mpulumutsi, pakutero iye amatsekereza mgwirizano ndi chiyanjano cha munthu ndi Khristu.

Pemphero losalekeza liri kulumikizana kwa uzimu wangwiwo ndi Mulungu, ndiponso njira yomwe m'phamvu ya moyo wochokera kwa Mulungu imafikira m'moyo wathu. Ichi chimachitika, nthawi iri yonse pamene ife tikupemphera kuti m'phamvu yakupatsa moyo imalowa mkati mwa moyo wathu. Pakutero moyo umakula wa m'phamvu “mwa Ambuye ndi mkulimba kwa m'phamvu yake” (Aefeso 6:10). Kukula kwathu mu chisomo, chimwemwe, kufunikira mu utumiki, zonse zidalira pa kulumikizana kwathu ndi Khristu. Ndi pakuyanjana ndi Iye, tsiku ndi tsiku, ora ndi ora; pakukhala mwa Iye pomwe ife timakula m'chisomo. Malingaliro ayenera nthawi zonse kumamfunafuna Mulungu. Tipemphere nthawi zonse. Tidalire pa Iye ora liri

lonse ndiponso mphindi iri yonse.

Tiwaphunzitse maganizo athu kuyang'ana kumwamba, ndi malingaliro athu kukhazikika pa Mulungu – ndi kuwaika kwa Iye kuchokera m'mawa mpaka usiku wonse. Pakutero padzakhalakulumikizana kwa ngwiwo ndi Mulungu, ndipo chiyanjano cha moyo wa chilunjiko ndi Ambuye chidzakwanitsidwa; ndipo chiyenera kusamalidwa ndithu. Munthu ali yense, kudzera mwa ntchito zake amalowa m'chijanano ndi Khristu kudzera pakudzikana, kukhulupirira komanso kumvera. Tiyenera ife kuugonjetsa undekha, kuzipachika pa mtanda zilakolako; ndi kuyamba kukhala pa ubale weni weni wa uzimu ndi Khristu. Ubale'wo ukakhazikitsidwa, ungate kupitirizika kusamalidwa, moonamtima ndi modzipereka nsembe kumbali yathu.

Iyi ndi njira yolandirira m'phamvu – pokakamira m'maganizo athu pa Yesu ndi kulimbika pakusungu chiyanjano chathu ndi Ambuye mwini moyo, kuunika, ndi m'phamvu. M'phamvu yake imafalikira m'moyo wathu, ndi kutipanga ife aphumphu. Pomlandira Khristu timaphimbidwa ndi m'phamvu yake. Kukhala kwa Khristu pakati pathu, kumapatsa m'phamvu, ndi kulimbikitsa moyo wathu wonse.

Pamene okhulupirira amakhala m'chilungamo cha Khristu amalandira m'phamvu yomwe imalowa ndi kukhazikika m'moyo wamkati.

Ndi chilungamo cha Khristu, khalidwe lake lopanda banga liri lonse la uchimo, lomwe kudzera mwa chikhulupiriro limapatsidwa kwa onse omwe amalandira Iye monga Mpulumutsi wao.

Kodi chilungamo cha Khristu ndi chiyani? Ndi khalidwe lopanda banga liri lonse la uchimo la Yesu.

Timachilandira motani chilungamo cha Yesu? Pomlandira Yesu kukhala Mpulumutsi wathu.

Mzimu Woyera adzawapanga onse omwe akufunitsitsa kuphunzira kuti athe kuchifalitsa choonadi ndi m'phamvu. Ndipo choonadicho chidzalenganso mwatsopano chiwalo chirichonse cha thupi lao, kuti atumiki a Mulungu athe kwigwira ntchito yao mobvomerezeka ndi mwachipambano. M'phamvu ya Umulungu imaonjezereka mwa munthu kudzera m'machitidwe a Mzimu Woyera.

“Mzimu utchedwa moyo chifukwa mwa uyu muli chilungamo.” Bukhu Lopatulika likutisindikama mwa pakunena, “Khristu...adzapatsanso moyo matupi anu mwa Mzimu wake wakukhala mwa inu” (Aroma 8:10, 11). M'mau awa Paulo akupitiriza ganizo lake lomwe lija la za chikhulupiriro:

“Koma ife tonse... popenyereka... ulemelero wa Ambuye, tisandulika m'chithunzithunzi chomwechi kuchokera kuulemelero kumka kuulemelero [monga] ngati kuchokera kwa Ambuye Mzimu” (2 Akorinto 3:18). Apa ganizo lija likupitirirabe kuphunzitsa momveka bwino kuti: ife timasinthika, “popenyereka ulemelero wa Ambuye.”

Anamwali asanu opusa akuimira guru lalikuru la anthu otaika. Kodi iwo ataika bwanji? Chifukwa iwo sadziwa momwe angakhulupirire Khristu, ndiponso angamuyang'anitsitsire kuti akhale ndi moyo. Komanso tikuuzidwa momveka bwino za chifukwa chimene



anamwali ena asanu aja adzapulumutsidwire, kudzakhalachifukwa chakuti anaphunzira kuyang'anitsitsa pa Khristu ndi kukhala ndi moyo atatha kuphunzira phunziro lofunikira kwambiri limeneli. Werengani Mateyu 25.

Ndi anthu okhawo omwe angakusamalire kuunika kwapang'ono komwe ali nako, omwense adzalandire kuunika kwakukuru. Ndi okhawo amene adzakhalamwachilungamo ndi m'phamvu yopatsidwa kwa iwo omwe adzalandira m'phamvu yochuruka. Padzakhalachoyamba m'mera, zidzatsatira ngale, pamenepo maso okhwima m'ngalemo” (Marko 4:28).

Momwe tingailandirire m'phamvu yochurukirapo zikudalira ndi momwe tinalandirira m'phamvu yocheperapo pachiyambi – titatansa manja athu kumkhuza Yesu, Iye amatipatsa m'phamvu yake, ndipo m'phamvu imenayo imanka ikuonjezekaonjezeka ngati titapitiriza kuikabe manja athu pa Iye. Chitsanzo ichi chimamveka bwino tikamakumbukira za mkazi uja analandira m'phamvu yamachiritso pamene anangokhuza mkawo wa chobvala cha Khristu. Khamu lalikuru lomwe linasonkhana momzungulira Khristu, silinaone m'phamvu ina iri yonse yomwe inachitika chifukwa cha kukhuzako. Koma pamene mkazi wosauka, wakumwa zowawa, wofunitsitsa kuchira uja, anangotansa dzanja lake kukhuza mkawo wa chobvala cha Yesu, anaimva m'phamvu yakuchiritsoyo ikulowa mwa iye. Kwake kunali kukhuza kwa chikhulupiriro. Khristu anukumva kukhuzidwako, ndipo

anaganiza zoti ili likhale phunziro kwa ophunzira ake onse, mpaka a kumapeto kwa nthawi kuno. Apatu panachitika kulekana kwa khukhuza wamba ndi kukhuza kwa chikhulupiriro. Kukhuza kwa chikhulupiriro kamatitsegulira ife chuma chobisika cha m'nyumbayosungiramo chomwe ndi m'phamvu ndi luntha za umulungu. Werengani Mateyu 9:20-22.

Choncho pomchiritsa mkazi uyu, Ambuye wathu anapereka chitsanzo cha momwe m'phamvu imapatsidwira. Ndi pomkhuza Iye kuti m'phamvu yakupatsa moyo imadza mwa munthu. Ndipo tikapitiriza kulumikizana ndi Iye m'phamvuyo imanka ikukulirakulira.

Pali kusiyana kwakukuru pakati pa chiyanjano chongodziyenerereza ndi chiyanjano cheni cheni cha kulumikizana ndi Khristu mwachikhulupiriro.

Tingathe ife kumvetsetsa za ubale wakulumikizana ndi Khristu monga ukufotokozedwa m'au awa, 'Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake' (Yohane 15:6). Kulumikizana kwa moyo, m'phamvu, ndi kubereka chipatso kuyambira kutunthu mpaka ku nthambi kudzikhalakwachikhilalire. Muzu umatumizira zakudya kudzera ku thambi. Umo ndimo udzikhalira ubale wotsimikizika pakati pa wokhulupirira ndi Khristu. Wokhulupirira adzikhalamwa Khristu ndikupeza zosowa zake mwa Iye. Timalandira chisomo kosalekeza kuchokera kwa Iye, ndipo Khristu amalandira kuyamika kuchokera kwa ife. Kulumikizana kwa mtundu uwo kukakhazikika, machimo athu amaikidwa pa Khristu, ndipo chilungamo chake chimapatsidwa kwa ife. M'phamvu ya uchimo imadzilumikiza kwambiri ndi chikhaliidwe cha umunthu koterokuti palibe munthu angathe kuigonjetsa, pokhapokha atalumikizana ndi Khristu. Chiyanjano cha m'chikhulupiriro cha moyo ndi Khristu chimakhala muyaya: pamene kulumikizana kwa mtundu wina kuli konse kumatha. Kulumukizana ndi Yesu umakhala mgwirizano wodalinka. Mgwirizano ndi Khristu ukakhazikitsidwa, ungate kusungidwa kudzera m'pemphero lotsimikiza mtima ndiponso kulimbika kosalekeza.

Kukhazikika kotheratu pa chikhulupiriro chathu kudalira pa chiyanjano chomwe tiri nacho.

Kusasinthika pa kulumikizana kwathu ndi Khristu ndi njira imene imaoonjezeka m'phamvu yake mwa ife. Uku kukufotokozedwa momveka bwino ndi Ambuyeyo m'chitsanzo chake cha mpesa ndi nthambi zake anachilankhulacho kasanu ndi kawiri momwe akulangiza “kukhala” mwa Iye: “Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu.

Monga nthambi siingathe kubala chipatso pa yokha, ngati siikhala mwampesa; motere mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine...Wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu. Ngati wina sakhala mwa Ine, watayika kunjja monga nthambi, nafota...Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akhala mwa inu, pemphani chimene chiri chonse muchifuna ndipo chidzachitika kwa inu" (Yohana 15:1-7).

Tikapitirira ife kukhala mwa Khristu, ngakhale Satana aponye patsogolo pathu zokhumudwitsa zoti zitichimwitse ndi cholinga chakuti ife tinyinyirike ndi kutukwana Mulungu ndipo pakutero tiotonge chiyanjano chathu ndi Iye, zimalephereka. Chikondi cha Ambuye chimaoneka pakukwaniritsa lonjezani lake, "Ngati mukhala mwa Ine...pemphani chimene chiri chonse muchifuna, ndipo chidzachitika kwa inu."

Kuti ife tizindikire chomwe choonadi chiri, tiyenera kuwerenga Malemo ndi kugwada maondo athu pansu, m'mawa, masana, ndi madzulo. Pemphero lochokera m'malo a mseri, ndiponso pemphero losalekeza, lochokera mkati mwa mtima mwathu liyenera kumaperekedwa kumwamba kuti Mulungu atitsogolere m'choonadi chonse.

"Kupemphera kosalekeza" kutsogolera kukulandira "mphamvu kosalekeza."

"Koma inu dikirani nyengo zonse, ndi kupemphera, kuti mulimbike kupulumuka zonse zimene zidzachitika, ndi kuimirira pamaso pa Mwana wa munthu" (Luka 21:36).

Dzanja la Mulungu ndi lokonzeka kupulumutsa anthu ake kuchokera ku zinthu zochita mwachizolowezi, motsutsana ndi Khristu monga unasokonekera mtundu wa Chiyuda; ndipo kuchepa machitidwe amene Mulungu anawalamulira kutsogolera kukukwaniritsa ichi, ndi chimodzimodzi kumkana Yesu. Moyo uli wonse womwe ufuna kupulumutsidwa uyenera kukhala pa chiyanjano ndi Mulungu mu ntchito yake ya chipulumutso; umunthu ndi umulungu ziyenera kulumikizana m'chikhulupiriro ndi mu ntchito. Ngati tifuna kuti tikhululukidwe, tiyenera ife kubvomereza ndi kulapa machimo athu, ndi kukhulupirira m'chikhululukiro cha Mulungu wa chifundo. Khristu, Mkuruwansembe wathu akuti, "Chisomo changa chikukwanira."

NDI YESU YEKHA MKURUWANSEMBE WATHU

Chikhristu ndi chipembedzo chokhacho mkati mwake muli

chipulumutso.

Ntchito yakuchilandira chipulumutso ndi imodzi yofunika m'gwirizano, ndi kuchitira zinthu pamodzi. Payenera kukhala mgwirizano pakati pa Mulungu ndi munthu wochimwa wofuna kupulumutsidwa. Iyi imafuna kukhazikitsidwa kwa machitidwe oyenera a khalidwe. Munthu ayenera kuchitapo mbali yake yakulimbana kuti agonjetse tchimo lomwe limamlepheretsa kukhala wangwiro. Ngakhale amafunika kuchita ichi ayenera iye kudalira kwatunthu pa Mulungu pa chipambano chake. Mphamvu ya munthu pa yokha siyokwanira. Popanda chithandizo cha mphamvu ya umulungu siingachite kanthu. Mulungu ayenera kutengako mbali pamene munthunso ayenera kutengakonso mbali. Kulikaniza tchimo kuyenera kuchokera kwa munthu, amene ayenera kupempha mphamvu yochokera kwa Mulungu kuti imthandize. Kumbali ina pafunika luntha, chifundo ndi mphamvu zochokera kwa Mulungu pamene kwinanso pafunika munthu kudzimva kuti ali ndi ufooko, kukuzindikira kuipitsitsa kwa uchimo, ndi kudzimva kuperewera kotheratu.

Ntchito kapena udindo wa mkuruwansembe ndi chimodzi cha zinthu zobvutitsitsa kuzifotokoza ndiponso zokhala ngati zosafunikira kweni kweni ku zimvetsetsa mu utumiki ndi m'chitidwe wa chikhristu. Cholinga chokhazikitsira mkuruwansembe ndi chakuti akhale m'khala pakati wa Mulungu ndi munthu. Mwa chibadwa chake munthu ndi wochimwa, wosayenera pamaso pa Mulungu, ndipo ndi wolekanitsidwa ndi Mulungu. Alibe mphamvu yakuyandikira kwa Mulungu, kapena njira yakutero, ngakhale atafuna ndikulalalaka kutero. M'malo mwake wochimwayo amangoganiza zothawathawa kuchoka pamaso pa Mulungu, ndi kusafuna kuyandikizana ndi Mulunguyo pa chiri chonse. Pakutero, iye amasowa kolowera kapena choti nkuchita kufikira papezeke munthu wina woti akhale womuimira wochimwayo kwa Mulungu. Panopa nkhoswe yokhaya yoimira pakati pa munthu ndi Mulungu ndi Ambuye Yesu Khristu Mkuruwansembe wathu.

Bukhu Lopatulika likuphunzitsa kuti, "Pakuti pali Mulungu mmodzi ndi Mtezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye munthu, Khristu Yesu" (1 Timoteo 2:5).

Utumiki wonse wa M'Chipangano Chakale wa unsembe wa chi – Levi umaimira nsembe ya Yesu ndipo unakhala ukugwira ntchito kufikira tsiku la imfa yake pa mtanda, ndi kung'ambika kwa chinsaru chotchinga

cha m'kachisi. Lero lino sizomveka kuti mpingo ungate kusungu unsembe koma nkumakana machitidwe ena omwe amayendera limodzi ndi m'chitidwe wa unsembe wa Chilevi.

Yesu Khristu anadza m'dziko lapansi kudzapulumutsa ochimwa. "Adzamutcha dzina lake Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ake ku machimo ao" (Mateyu 1:21). Zikuoneka kuti palibe funso lakuya liri lonse lomwe lingafunsidwe m'chipembedzo kuposa ili lakuti, kodii zinatheka bwanji?


Mosachita kukaika konse, mipingo iri ndi njira zomwe imazigwiritsa ntchito kutontholetsa chikumbumtima chao, ndipo iyo imazigwiritsa ntchito njira zomwe muli chikunja pang'ono ndipo zomvetsa chisoni. Njira zimene iwo amazifuna ndi zokhala ndi machitidwe oiwalitsa Mulungu koma amazigwiritsa ntchito kukhala ngati zokumbukirira Iye. Pali magulu awiri a anthu omwe aziphunzitsa zolakwika m'dziko lonse lapansi: gulu lomwe limati lidzapulumutsidwa mwa ntchito zao ndi lina lomwe limati lidzapulumutsidwa liri chikhaliro m'machimo (lingathe kumachitabe machimo kufikira kudza kwa Yesu). Panopa magulu onse awiri a ziphunzitsa zolakwika wa akulandiridwa m'mpingo.

Koma Paulo akufotokoza momwe munthu angakhaliro wangwiro ndi momwe zingathekere. "Gwirani ntchito ya chipulumutso chanu," akutero iye, "pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe...ndiye Mulungu" (Afilipi 2:12, 13).

"Pakuti mau a Mulungu ali amoyo, ndi ochitachita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napoyza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima. Ndipo palibe cholengedwa chosaonekera pamaso pake, koma zonse zikhala za pambalabanda ndi zobvundukuka pamaso pake pa Iye amene tichita naye. Popeza tsono tiri naye Mkuruwansembe wamkuru, wopoyza miyamba, Yesu Mwana wa Mulungu, tigwiritsitse chibvomerezo chathu. Pakuti sitiri naye m'kuru wa nsembe wosatha kumva chifundo ndi zofoka zathu; koma wayesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda uchimo. Potoero tilimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa" (Ahebrei 4:12-16).

Ndi mau awa mtumwi Paulo akuonetsera chisamaliro ngakhale cha zinthu zochepetsa kwambiri komanso udindo umene waperekedwa

ndi Mkuruwansembe wamkuru yemwenso ndi Mkuruwansembe – Mlengi pa ana a anthu. Iye, pokhala Mau a Mulungu ali lupanga lakuthwa konse konse, amalekanitsa zinthu zomwe zimaoneka zobvutitsitsa kuzigawanitsa kapena kuzisiyanitsa. Amadziwa za m'maganizo, komanso kuyeza cholinga cha zochitika zonse. Umu ndimo



mtumwi wogwidwa ndi Mzimu akufotokozera ntchito ndi utumiki za Ambuye wathu Yesu Khristu monga Mkuruwansembe.

Chiphunzitsa cha choonadi chofunikira'chi chikufotokozedwa m'bukhu la Chibvumbulutsu 1:11-20).

M'bukhu ili Ambuye wathu akufotokozedwa mu udindo wake wakukhala Mkuruwansembe, ndipo patsogolo asanadzionetsere kuti ali Mkuruwansembe m'kachisi akuyendayenda pakati pa zoikapo nyale zisanu ndi ziwiri (Chibvumbulutsu 1:11-20). Ambuye wathu akudzifotokoza kuti, "Ine ndine Wamphamvuyonse" (Chibvumbulutsu 1:8). Ndipo atatha kudzifotokoza kuti ali Mkuruwansembe – Wamphamvuyonse, akunena kwa uliwonse wa mipingo isanu ndi iwiri, "Ndidziwa ntchito zako" (Chibvumbulutsu 2 ndi 3). Kudziwa uku sikunali kwa nthawi yomwe ija yokha koma ngakhale kobvutitsitsa kwa mtsogolo, chifukwa Yohane anaitanidwa ndi Ambuye wathu Yesu namuonetsa iye, "zimene ziyenera kuchitika m'tsogolomo" (Chibvumbulutsu 4:1). Apa Ambuye wathu anabvumbulutsira Yohane za zinthu zimene zinali kudzachitikirira mpingo mtsogolo. Kumayambiriro kwenikweni kwa zochitikirira mpingo Ambuye anamuonetsera Yohane, kukupindula kwa mibadwo yamtsogolo, kuti zodzachitika m'tsogolo zonse zinali kwa Iye monga bukhu lotsegula lomwe

anawerengamo, ndipo panalibe chom'bisikira chiri chonse, ndi kuti palibe chiri chonse chodzauchitikira mpingo mtsogolo chidzakhala chomdabwitsa ndi kumdizidzimutsa. Choncho mpingo unayenera kukhala wodzala ndi chimwemwe ndiponso chitonthozo m'chidziwitso chakuti chinthu chiri chonse chodzauchitikira chinadziwika kale ndi Ambuye Wamkuru wa mpingowo, ndipo kuti lye anaika kale njira zoupulumutsira m'nthawi za masautso. Kwa Yohane kunabvumbulutsidwa adani onse a mpingo; mazunzo ndi zisautso zonse zomwe udzadzutsamo, kuphatikiza za mkangano wotsiriza pamapeto peni peni pa nthawi ya pansu pano womwe udzakhaza Sabata.

Kwa Yohane kunaonetsedwa zinthu za chinsinsi ndi za kuya zochititsa chidwi chachikuru zomwe mpingo unali kudzadzutsamo. Anaonetsedwa momwe adzachitire oyera mtima, zoopsya, mikangano, komanso mapeto akupulumutsidwa kwa anthu a Mulungu. Zinthu zazikuru ndi zofunikira kwambiri zinabvumbulutsidwa kwa iye, makamaka zokhuza utumiki wotsirizira wa mpingo wakumapeto.

Chiphunzitso cha Bukhu Lopatulika chakuti maso a Mulungu amayang'ana pa ife nthawi zonse sichikuperekedwa munga chenjezo (ngakhale kwa ochimwa chiyenera kukhala chenjezo). Chiphunzitsochi chikuperekedwa momveka bwino m'Mau a Mulungu'wo munga chilimbikitso kwa anthu a Mulungu; ndiponso chifukwa n'chofunikira kwambiri pakukhala m'chikhristu. Mpfundo iyi iyenera kusungidwa ndi onse ofunitsitsa kulandira chilungamo mwa chikhulupiriro – sichikhulupiriro chokhacho chomwe munthu ayenera kukhala nacho pangodziganizira mwa iye yekha, kapena chinthu chimene wina ayenera kungochilingalira kokha; koma ndi chiphunzitso chomwe tiyenera ife kuzindikira za kufunikira kwa kuchitapo kanthu kwathu kuti chikutitsogolera kuchidziwitso chakuti kukhala olungamitsidwa mwa chikhulupiriro ndi khalidwe lochitidwa posinthanitsa ukale ndi umunthu wathu watsopano. Sipangakhale kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro ngati palibe chidziwitso ichi chochitsitsimutsa chikumbumtima cha uzimu wathu mphindi iri yonse ya pa tsiku. Apatu ndi pomwe ambiri timalepherera kulimvetsetsera tanthauzo leni leni la kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro.

Mphamvu yaikuru chotani yomwe Mulungu ali nayo kuti akutha kuyang'anira munthu ali yense wokhala pa dziko lapansi, ndikudziwa zolingirira

za m'moyo uli wonse, kumva, kuona chochitika chiri chonse, kuti athe kupereka chiweruzo cha chilungamo pa nthawi yake ndiponso cha tsiku ndi tsiku pa zochita za munthu ali yense, komanso kuyang'aniranso unyinji wosawerengeka wa maiko, ndi madzuwa omwe amayenda mosaphophonya m'njira zao! Ndi choonadi chozizwitsa ndi "chodabwitsa" ichi chomwe chinampangitsa Davide kulemba,

“Munandisanthula, Yehova, nimundiziwa, Inu mudziwa kukhala kwanga ndi kuuka kwanga, muzindikira lingaliro langa muli kutali. Muyesa popita ine ndi pogona ine, njira zanga zonse muzolowerana nazo. Pakuti asanafike mau pa lilime langa, taonani, Yehova, muwadziwa onse. Munandizinga kumbuyo ndi maso, Nimunaika dzanja lanu pa ine. Kudziwa ichi kundilaka ndi kundidabwitsa; kundikhalira patali, sindifikirako. Ndidzapita kuti kuzemba m'zimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kuzemba nkhope yanu?”

Atatha kufotokoza kuti kuli konse kumene amapita akupeza kuti Mulungu ali komweko, ndipo kuti Mulunguyo amadziwa makulidwe ake kuyambira asanabadwe kufikira kukula kwake, Davide akunenanso,

“Potero, Mulungu, ndiziyesa zolingilira zanu za mtengo wake ndithu! Mawerengedwe ake ndi ambirimбири! Ndikawerenga zichuruka kuposa m'changa: ndikauka ndikhalanso nanu” Masalmo 139:1-18).

Yesu, Wamkurwansembe wathu, ayenera kupezeke paliponse munga Mulungu Atate, ngati siziri choncho sizingathekensho lye kutumikira munga Mtezi za munthu pamaso pa Atate wopezeke paliponseyo. Zifundo zonse ndi madalitso a Mulungu zimadzera mwa Yesu. Ichi n'chifukwa chake Yesu anakhala akunena za kukhala mmodzi kwake ndi Atate kambirimбири. Iye anati, “Zinthu zonse zinaperekedwa kwa Ine ndi Atate wanga; ndipo palibe munthu adziwa Mwana koma Atate yekha; ndi palibe wina adziwa Atate, koma Mwana yekha, ndi iye amene Mwana afuna kumuululira. Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumultsani inu” (Mateyu 11:27, 28). “Ine ndine njira choonadi ndi moyo: palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine” (Yohane 14:6). “Ine ndine khomo; ngati wina alowa ndi Ine, adzapulumutsidwa, nadzalowa, nadzaturuka, napeza busa” (Yohane 10:9).

Kuchokera m'ndime izi ndi zina zopezeke m'Bukhu Lopatulika tikuona kuti nkofunikira kwambiri kuti ife twigwiritsitse chiphunzitso chofunikira

kwambiri cha chikhristuchi choti chipulumutso chathu chidalira pa lye amene ali Mkurwansembe wa pa malo ponse, amene ndi Ambuye wathu Yesu yemwe akunenanso, “Pakuti ngati simukhulupirira kuti INE NDINE, mudzafa m'machimo anu” (Yohane 8:24). Pokhapokhapo tikhulupirire kuti lye ndi INE wamkuru wa M'Chipangano Chakale, Mulungu wopezeke pali ponse yemwe analenga dziko lapansi ndi kukhala ndi anthu ake m'mibadwo yonse, “tidzafa ife m'machimo athu.” Chiyembekezo chathu chokhacho chakuti n'kugonjetsa nacho tchimo chiri pakukhulupirira kukhala M'modzi kwake ndi Mulungu ndi kubvomereza kuti mphindi iri yonse lye akugwiritsa ntchito Umphamvuyonse wa Atateyo m'zonse zimene amatitsogolera kuzichita, kuziganiza kapena kuzilankhula, ngati tikupitirirabe kuyang'ana pa lye.

“Potero, abale oyera mtima, olandirana nao maitanidwe akurwamba, lingirirani za Mtumwi ndi Mkurwansembe wa chibvomerezo chathu Yesu Khristu” (Ahebi 3:1). Mpfundo ziwiri izi zakuti Yesu anatumidwa ku dziko lapansi'li ndi Atate wake kudzakhala woimira Umodzi wa Mulungu kwa munthu ndikutinso anakwera kumwamba kukhala woimira munthu ku mpando wachifumu wa Mulungu – n'zosalekanitsika: ndi ziphunzitso ziwiri zokhala ndi cholinga chimodzi. Ndi Mulungu – Munthu yekha amene akutha kukhala pa mpando wa chifumu wa Mulungu. Ichi n'chiphunzitso chofunikira kwambiri ndi choyenera kumaphunzitsidwa mobwereza-bwereza, chifukwa ngati sipangakhale kuigawa ndi kupatsa mphamvu ya Atate kosalekeza kudzera mwa Mkurwansembe palibe munthu ndi m'modzi angakhale m'moyo wa chikhulupiriro cha chikhristu. Chilungamo chakuchitidwa mwa chikhulupiriro ndicho kuigwiritsa ntchito Mphamvuyonse ya Yesu pakukhala m'moyo wa chiyero. Sipangakhale chinthu chotchidwa chilungamo chakuchitidwa mwa chikhulupiriro ngati sifingamalandire mphamvu yochokera kukasupe wosaphwaya.

Yesu anapemphera, “Atate Inu, lemekezani Ine...ndi ulemelero umene ndinali nao ndi Inu lisanakhale dziko lapansi” (Yohane 17:5). Tikhulupirire ndithu kuti lye amene anatumizidwa sanali wina koma Mwama wa Mulungu, Mlengi wa zonse. Choncho Uthenga Wabwino wa Yohane ukuyamba ndi choonadi choposachi, “Pachiyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu. Awa anali pachiyambi kwa Mulungu. Zonse zinalengedwa ndi lye; ndipo

kopanda lye sikukukanalengedwa kanthu kali konse kolengedwa...Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemelero wake, ulemelero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi” (Yohane 1:1-3, 14).

Uthenga Wabwino wa Yohane, munga tikudziwa bwino, unalembedwa pofuna kuonetsera Umulungu wa Ambuye wathu, ndipo chiri chonse chomwe chalembedwa m'menemo chiri umboni wa choonadi chopambana ichi. Yesu anafotokozanso kuti ntchito zake zinachitira umboni kuti ali Mulungu (Yohane 10:25, 32, 36-39). Munga kwafotokozedwanso m'ndimezi, Ayuda anafuna kumgwira lye chifukwa amati lye anachitira mwano Mulungu... Pakudzifotokoza kuti lye anali m'modzi m'maonekedwe, chikhaliidwe ndi machitidwe munga anali Atate wake, Yesu anati, “Mukadazindikira Ine

Mwa umunthu wake, Khristu anadzilunzanitsa ndi mtundu wa anthu; mwa Umulungu wake, akulunzanitsidwa ndi mpando wachifumu wa Mulungu. Pokhala Mwana wa munthu, anatisiyira ife chitsanzo chakumvera; ndipo pokhala Mwana wa Mulungu anatipatsa ife mphamvu yakumvera. Ndi Khristu yemwe analankhula kwa Mose kuchokera muchitsamba m'phiri la Horebe kuti, “INE NDINE YEMWE NDIRI INE...Ukatero ndi ana a Israyeli, INE NDINE wandituma kwa inu.” Eksodo 3:14. Ili linali pangano la maombolede a ana a Israyeli. Ndipo pamene lye anadza, “nakhala m'mafanizidwe a anthu,” Anadzitcha INE NDINE. Mwana waku Betelehemu, Mpulumutsi wofatsa ndi wodzichepetsa, ali Mulungu yemwe “anaonekera mthupi.” 1 Timoteo 3:16. Ndipo kwa ife Iye akauti, “NDINE Mbusa Wabwino.” “NDINE Mkathe wamoyo.” “NDINE Njira, Choonadi ndi Moyo.” “Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi dziko lapansi.” Yohane 10:11; 6:51: 14:6; Mateyu 28:18. NDINE chitsimikizo cha pangano liri lonse. NDINE musaope. “Mulungu nafe” ali maziko a maombolede athu kuchokera ku uchimo, chitsimikizo cha mphamvu yathu ya kumvera ndi kusunga lamulo la kumwamba.

mukadadziwa Atate wanganso; kuyambira tsopano mumzindikira Iye, ndipo mwamuona Iye...Iye amene wandiona Iye waona Atate" (Yohane 14:7-11).

Utumiki wonse wa zinsembe zopahira womwe unali kuimira Khristu unapita; pa nthawi iyi maso a anthu anali nkuona nsembe yeniyeni yoona yoperekedwa chifukwa cha machimo a dziko lapansi. Utumiki wa ukuruwansembe wa dziko lapansi unatha; koma tsopano tikuyang'ana kwa Yesu, Nkhoswe ya chipangano chatsopano, ndi "kwa mwazi wa kuwaza wakulankhula chokoma choposa mwazi wa Abele." "Koma atafika Khristu, Mkuuwansembe wa zokoma zirinukudza, mwa chihema chachikuru ndi changwiwo choposa, chosamangika ndi manja...mwa mwazi wa Iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika atalandirapo chiombolo chosatha cha Iye" Ahebr 12:24; 9:11-12) KJV. "Kuchokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye, popeza ali nao moyo wake chikhaliye wakuwapembedzera iwo" (Ahebr 7:25).

Pakunena za Ukuruwansembe, ndi Khristu yemwe ndi Wansembe wathu, Mkuuwansembe wathu yekhayo. Iye akukwanitsa kukhala wotero chifukwa anadziperereka Mwini yekha nsembe yakukwaniritsa chilungamo nachititsa zinsembe zina zonse kukhala zosafunikiranso. Iye analipira dipo la machimo a anthu ake, pakutero natsegula njira ya chiyanjano chatsopano pakati pa anthuwo ndi Mulungu. Ndipo pakupitirizabe kukhala Mpulumutsi woukutsidwayo ndi wokwezewa wa anthu ake akuwapembedzera kosalekeza iwo kwa Mulungu Atate.

Zonse'zi zalembedwa momveka bwino ndi mlembi wa Kalata yaku Ahebr 1 yemwe pa mutu wachisanu ndi chinai akuti, "Koma atafika Khristu, Mkuuwansembe wa zokoma zirinukudza, mwa chihema chachikuru ndi changwiwo choposa, chosamangika ndi manja, ndiko kunena kuti, chosati cha chilengedwe ichi, kapena mwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe, koma mwa mwazi wa Iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo chiombolo" (Ahebr 9:11-12), kuti ife tiomboledwe kudzera mu "mwazi wa Khristu amene anadziperereka yekha wopanda chirema kwa Mulungu" (ndime 14); ndipo "sanalowa m'malo opatulika omangika ndi manja, akutsanza oonawo; komatu m'Mwamba momwe, kuonekera tsopano pamaso pa Mulungu chifukwa cha Iye" (ndime 24); kuti "tsopano kamodzi pa chitsiriziro cha

nthawizo waonekera kuchotsa uchimo mwa nsembe ya Iye yekha" (ndime 26); kuti pa Ahebr 8:1, 2, tithe kunena, "Tiri naye Mkuruwansembe wotere, amene anakhala pa dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Ukuru m'Kuwamba, Mutumiki wa malo opatulika, ndi wa chihema choona, chimene Ambuyee anachimanga si munthu ai."

"Koma ngati tiyenda m'kuunika, monga Iye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzake, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse.

"Ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutsambitsa kutichotsera chosungama chiri chonse" (1 Yohane 1:7, 9). Kukhululukidwa ndi kuyeretsedwa zimachitika mwa chisomo.

"Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi sichichokera kwa inu: chiri mphatso ya Mulungu" (Aefeso 2:8). Pakukhala m'chijanano ndi Khristu, akhristu ali afulu kufika kwa Mulungu nthawi zonse. Ufulu uwu ndi chinthu chimodzi cha zinthu zofunikira kwambiri m'chikhulupiriro cha mkhristu ndiponso choyenera kukhala nacho nthawi zonse. Bukhu Lopatulika likutiitanira ife kudza kwa Mulungu mwa Khristu, popanda kudzera kwa ansembe kapena amkhalapakati ali wonse a umunthu.

Unsembe wakutetezera womwe umadziwika m'Chipangano Chatsopano ndi wa Khristu, Mkuuwansembe wamkuru, ndipo ndi kwa yekhayo kuyenera kuperekedwa udindo wakuti "wansembe" (hiereus): "Iwe ndiwe wansembe nthawi yosatha monga mwa dongosolo (osati la unsembe wa Chilevi wa m'Chipangano Chakale koma) la Melikizedeke" (Ahebr 7:17); "Koma Iye chifukwa kuti akhala Iye nthawi yosatha ali nao unsembe wosasinthika, kuchokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye, popeza ali nao moyo wake chikhaliye wa kuwapembedzera iwo. Pakuti mkuru wa ansembe wotere anatiyenera ife, woyera mtima, wopanda choipa, wosadetsedwa, wosiyana ndi ochimwa, wakukhala wopitirira miyamba; amene alibe chifukwa cha kupereka nsembe tsiku ndi tsiku monga akuru a ansembe, yoyambira chifukwa cha zoipa za iwo eni, yinayi chifukwa cha zoipa za anthu; pakuti ichi anachita kamodzi, kwatha, podzipereka yekha" (Ahebr 7:24-27).

Paulo akufotokoza za mautumiki ndi maudindo osiyanasiyana m'mpingo wa chikhristu, ndipo udindo wa unsembe sanauke pakati pa awa: "Ndipo Iye

anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa; ndi ena aphunzitsi" (Aefeso 4:11). Komanso "Ndipotu Mulungu anaika ena m'Elesia, poyamba atumwi, achiwiri aneneri, achitatu aphunzitsi. ..." (1 Akorinto 12:28).

"Chifukwa chake mubvomerezane wina ndi mnzake machimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzake kuti muchiritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'machitidwe ake" (Yakobo 5:16).

MULUNGU ADZAKHALA NDI ANTHU OYERA MTIMA

Kuti akampatule, atamyeretsa ndi kumsambitsa madzi ndi mau; kuti akadziikire yekha mpingo, wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyera, ndi wopanda chirema. (Aefeso 5:26, 27).

Lero lino mudzipereke kwa Mulungu, kuti Iye akupangeni chotengera cha ulemu, choyenera ntchito yake. Lero lino mudzipereke kwa Mulungu, kuti muchotsedwe undekha, muchotsedwe kaduka, nsanje, malingaliro oipa, matetano, ndi chinthu china chiri chonse chochititsa Mulungu mwano. Lero lino mubvomereze kutsukidwa kuti mukhale ndi moyo woyera wokonzeka kulandira madalitso akumwamba, kulandira mvumbi wa Mzimu Woyera, womwe unalonjezedwa kuti udzaperekedwa, ndiponso madalitso a Mulungu omwe adzadzadza moyo woyeretsedwa kuchokera kuchibvundi. Ndi udindo wathu pano kupereka miyoyo yathu kwa Khristu, kuti atiyenereze kukhala okonzeka kulandira nyengo zakutsitsimutsa zochokera pamaso pa Mulungu.

Tizindikire kuti mphamvu ya umulungu ikagwirira ntchito limodzi ndi ya umunthu, ntchito ya uthenga idzafalikira ngati moto paudzu wouma. Choncho nkofunika kwambiri kuti Mulungu adzikhala ndi atumiki a umunthu m'munda wake pokwaniritsa zomwe zalembedwa m'Malemo - ... "ndipo dziko lapansi linaunikidwa ndi ulemelero wake." (Chibvumbulutso 18:1). Khalidwe la Mulungu ndilo ulemelero wake, choncho atumiki ake a umunthu ayeneranso kulionetsera ilo, lomwe ndi chikondi ndi chilungamo cha Yesu. Kodi Yesu akudikira inu kapena ine?

Pamene ntchito ya Mulungu ikunka kumapeto, magwiridwe olimbika ochitidwa ndi okhulupirira opatulidwa mwapadera motsogozedwa ndi Mzimu Woyera, ayenera kukwanitsidwa pophatikizana mwapadera ndi mphamvu ya umulungu. Kumapeto kwa nthawi kuno mphamvu ya Mzimu

Woyera ipatsidwa mu mpingo woona.

Ndi anthu otani omwe akupanga mpingo woona? Bukhu Lopatulika likupereka mafotokozedwe awiri a chidule a iwo amene akupanga mpingo woona m'nthawi yakumapeto ino.

Ndipo chinjoka chinakwayiwa ndi mkazi, (mkazi = mpingo) nichichoka kunka kuchita nkondo ndi otsala a mbeu yake, amene asungu malamulo a Mulungu, nakhala nao umboni wa Yesu. (Chibvumbulutso 12:17).

Pano pali chipiriro cha oyera mtima; pano [pali] iwo akusungu malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu. Chibvumbulutso 14:12.

Padzakhala anthu oyera mtima. Yesu akutsimikizira ganizo'li, "Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao." (Mateyu 18:20). Choonadi n'chakuti Mulungu ali ndi mpingo. Si nyumba yaikuru yopemphereramo, kapena bungwe lokhazikitsidwa ndi pfuko la anthu kapena mipingo yosiyanasiyana yomwe tikuidziwayi; koma ndi anthu omwe amamkonda Mulungu ndi kusungu malamulo ake. "Pamene anthu awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao." Pamene Khristu amapezeka, ngakhale pakati pa anthu odzichepetsa



ochepetsetsa, amapanga mpingo, chifukwa ngakhale Wam'mwambamwambayo ndi Woyera Yekhayo amene akhalitsa ku nthawi zonse mwa Iye yekha akupanga mpingo.

Pamene pamapezeka awiri kapena atatu okonda ndi kumva malamulo a Mulungu atasonkhana pamodzi, Yesu amakhala pomwepo, kaya kutali m'nkhalango za dziko lapansi,

m'chipululu, m'mizinda ndiponso mkati mwa nyumba za ndende. Ulemelero wa Mulungu umapyola makoma a nyumba za ndendezo ndikupereka kuwala kochokera kumwamba m' zipinda za mdima wandiweyani za pansi pandenze. Anthu ake oyera mtima angathe kuzunzidwa, koma mazunzo ao munga anachitira a atumwi akale, adzathandizira kufalitsa chikhulupiriro chao ndi kupindulira miyoyo kwa Yesu komanso kukweza dzina lake loyera. Kulimbana koopsy komwe kukuchitidwa ndi otsutsana ndi malamulo a muyaya omwe ndi muyeso wa chilungamo cha Mulungu kusatigwetse mphwai ndipo kusadzagwedzenso chikhulupiriro cha iwo odalira pa Mulungu kotheratu mtsogolo'mu.

Iwo amene akuchita mau akuphunzitsidwa ndi kulimbikitsidwa mwapadera, ndipo namondwe ndi mazunzo za chizunzo zidzagwetse makunzo pomwe iwo akhazikikapo, chifukwa miyoyo yao yakhazikika pa Thanthe lakunthawi zosatha.

M' masomphenya ake akufotokoza za zomwe zidzawachitikira amitundu pakupita kwa nthawi, Danieli akonetseranso chithunzi cha zochitika za kumapeto a dziko lapansi –

Ndipo nthawi yomweyi adzauka Mikayeli kalonga wamkuru wakutumikira ana a anthu a mtundu wako; ndipo padzakhala nthawi yamasautso, siinakhala yotere kuyambira mtundu wa anthu [ngakhale] kufikira nthawi yomwe ija; ndipo nthawi yomweyo anthu ako adzapulumutsidwa, yense amene ampeza wolembedwa m'bukhu.

Ndipo ambiri a iwo ogona m'pumbi lapansi adzauka, ena kuma ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozo wosatha.

Ndipo aphunzitsi adzawala ngati kunyezimira kwa thambo; ndi iwo otembenuza ambiri atsate chilungamo ngati nyenyezi ku nthawi za nthawi. (Danieli 12:1-3).

Paulo ndi atumwi anzake anagwira ntchito nthawi ya chizunzo. Choncho oyera mtima nawonso ayembekezere chizunzo kumapeto a nthawi. Kodi Paulo akutipatsako malingalilo a momwe tingadzachitire ndi chisautso munga chinachitikira kwa iwo kale, munga chinauchitikira mpingo woyambawo ndipo chidzateronso ku mpingo wotsala? Inde, akutipatsa!

Chotsalira, abale anga, tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi m'kulimba kwa mphamvu yake.

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kuchirimika pokana machenjerero a mdierekezi.

Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukuru, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a choipa m'zakumwamba.

Mwa ichi mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima chitsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutachita zonse, mudzachimika.

Chifukwa chake chirimikani, mutadzimangirira m'chiuno mwanu ndi choonadi, mutabalanso chapachifuwa cha chilungamo; ndipo mutadzibveka mapazi anu ndi makonzedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere;

Koposa zonse mutadzitengeranso chikopa cha chikhulupiriro, chimene mudzakhoza kuzima nacho mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo.

Mutengenso chisoti cha chipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu;

Mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo pochezera pamenepo chichezerere ndi kupembedzera oyera mtima onse,

Ndi ine ndemwe, kuti andipatse mau m'kunditsogulira m'kamwa molimbika, kuti ndizindikiritse anthu chinsinicho cha Uthenga Wabwino. Aefeso 6:10-19)

Mzimu wa Wamphamvuyonse ukuyenda pakati pa mitima ya anthu, ndipo onse amene akubvomera chifuniro chake akukhala mboni za Mulungu ndi za choonadi chake.

M'malo ambiri amuna ndi akazi opatulidwa akupezeka akalalikira kwa ena kuunika komwe kukuwatsegula olalikidwawo maso kumvetsetsa za njira ya chipulumutso kudzera mwa Khristu. Ndipo momwe akunka akukonetsera kuunika kwao, munga anachitira anthu amene anabatizidwa ndi Mzimu Woyera pa tsiku la Pentekoste, olalikirawo akunka akulandira mphamvu ya Mzimuyo yomwe ikunka ikukulirakulira mwa iwo. Ndipo kumapeto kwake dziko lapansi liunikidwa ndi ulemelero wa Mulungu.

Koma pafupi peni peni pa kutsekedwa kwa kholora la dziko lapansi, mphamvu yapadera ya chisomo cha uzimu wopambana ikulonjezedwa kuti idzakonzetsere mpingo za kubwera kwa Mwana wa munthu.

Tsiku ndi tsiku atumiki a Mulungu'wa akunka akukulirakulira m'chisomo cha utumiki wao chomwe akutha kuchifikiracho. Tsiku ndi tsiku akalalikira za Ambuye pena paliponse pomwe ali, kulalikira m'khalidwe m'mabanja ao kapena kulalikira ku makamu a anthu.

M'mawa uli wonse, iwo munga amithenga a Uthenga Wabwino amagwada pamaso pa Ambuye

ndikukonzanso mapangano ao akudzipatulira kwa lye mwatsopano, kuti lye apitirize kuwapatsa mphamvu ya Mzimu wake, yomwe imadzetsa chitsitsimutso ndi mphamvu yakuyeretisa. Ndipo akamayamba kugwira ntchito yao ya tsiku ndi tsiku, amalandira chitsimikizo chakuti Mzimu Woyera wosaonekayo ali pakati pao ndi kuwalimbikitsa kukhala antchito anzake ndi Mulungu.

Machitidwe ali onse a ntchito zosayenera, kudzikonda kuli konse zimachotsedwa ndi mphamvu yopatsidwa kwa iwo ya Mzimu Woyera. Chilakolako cha mafano chimachotsedwa. Gome liri lonse la nsembe za mafano limagwetsedwa kupatula gome lokhalo pomwe pamalemekezedwapo mpatso ndi lye wakuipereka – ya nsembe ya pamtanda pa Gologotha.

Tiyeni tigwire ntchito ali yense payekhapayekha. Tipemphere kwambiri ndi kuchepetsa kulungolora zopanda pake.

Monga zafotokozedwa kale pamwambapa, ndi okhawa amene akukugwiritsa ntchito kuunika kochepa komwe analandira omwe adzalandira kuunika kwakukuru koonjezera. Pokhapokhapo tikhale tikukula m'moyo wathu wachikhristu tsiku ndi tsiku ndi kudzipatula, sitingathe kuimvetsetsa ntchito yomwe Mzimu Woyera akuchita pakati pathu. Ingathe kumachitika tikuiona, koma osaizindikira ndi kulandira.

Iwo amene sakuchitapo kanthu koma akungoyembekezera kuti Mzimu Woyera ndiye awauze choyenera kuchita, adzataika ku mdima wakunja. Sitiyenera ife kungokhala osachitapo kanthu mu ntchito ya Mulungu. Ngati iwo odzitcha anthu a Mulungu sakuchitapo kanthu pakulapa ndi kubvomereza machimo ao, kukonza makhalidwe ao ndi kusiya ntchito zoipa za thupi ndi za uzimu zomwe, adzapezedwa osakonzeka.

Pasakhale munthu wodzinamiza kuti chifukwa amapita ku nyumba zopemphererako, ndiye kuti wakwaniritsa utumiki wake. Si chiphunzitsi cha mau osasinthika a Mulungu kuti iwo osonkhana pamodzi kaya m'magulu akuru kapena ang'ono adzalandira madalitso ochuruka kuchokera kumwamba.

Pamene ziwalo za mpingo wa Khristu zidziyandikira nthawi ya kulimbana kwao kotsiriza, "nthawi ya masautso, siinakhala yotere kuyambira mtundu wa anthu," adzazikika mwa Khristu, nalandira gawo lalikuru la mzimu wake. Pamene chenjezo lotsiriza lidzafalikira pa dziko lapansi, ndipo

mphamvu ndi ulemelero za Mulungu zidzatenga gawo lalikuru kukutsekera kwa ntchito, anthu okhulupirika a Mulungu adzabvekedwa ulemelero. Uku kudzakhala kuperekedwa kwa mphamvu ya Mzimu Woyera yomwe idzadzetsa chitsitsimutso ndi kuwalimbikitsa iwo kudutsa mosachita mantha mu nthawi ya chisautso irinkudzayo, yomwe mkati mwake mudzakhala yesero lotsiriza patso golo pa, "lye (Yesu) Wamoyoyo ndipo anali wakufa...ndipo ali nazo zofungulira za imfa ndi hade" (Chibvumbuluto 1:18) asanatsegule manda a olungama akufa. "Pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo kukakomana ndi Ambuye m'lengalenga: potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." (Werengani 1 Atesalonika 4:16, 17).

Pakuti chionekera chisomo cha Mulungu chakupulumutsa anthu onse, ndi kutiphunzitsa ife kuti, pokana chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m'dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza; akulindira chiyembekezo chodala, ndi maonekedwe a ulemelero wa Mulungu wamkuru ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu; amene anadziperaka yekha m'malo mwa ife, kuti akatiombole ife ku zoipa zonse, nakadziyeretsere yekha anthu akhale ake eni eni, achangu pa ntchito zokoma. Izi lankhala, ndipo uchenjeze, nudzudzule ndi ulamuliro wonse. Munthu asakupeputse. (Tito 2:11-15). Alemekizeke Mulungu!

LIMODZI LA MAITANIDWE OTSIRIZA A KHRISTU KWA ANTHU AKE

Ulosi wa Chibvumbuluto 16:13-16 ukufotokoza za kulimbana kotsiriza pakati pa mphamvu za chilungamo ndi za chisalungamo; ukuonetseranso chenjezo lokhalo lotsiriza la Khristu kwa anthu ake kuti akhale "atadzibveka mwinjiro" wa chilungamo chake kukonzekera za mkangano wotsiriza. Palinso kuitanira kwina koperekedwa kwa anthu a Mulungu m'Chibvumbuluto 14:6-12 ndi Chibvumbuluto 18:4.

Chingakhale chinthu cha nzerunso kufotokoza mwachidule ndime izi zokhuzo nkondo yaikuru yotsiriza yeni yeni, yotchedwa Harmagedo.

"Ndipo ndinaona moturuka [kuchokera] m'kamwa mwa chinjoka, ndi m'kamwa mwa chirombo ndi m'kamwa mwa mneneri wonyenga [kulankhala ngati ali amodzi] mizimu itatu yonyansa, ngati achule (achule amalira molandizana).

Pakuti ali mizimu ya ziwanda

zakuchita zizindikilo; zimene [zomwe] zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse, [pano pali mgwirizano wa zandale ndi zachipembedzo – womwe posachedwapa mipingo iugwiritse ntchito yakukhazikitsa malamulo opondereza choonadi] kuwasonkhanitsira ku nkondo ya tsiku lalikuru la Mulungu Wamphamvuyonse [yakulimbana ndi Mulungu pakuzunza oyera mtima].

(Taonani, ndidza ngati mbala. Wodala iye amene adikira, nasunga zobvala zake, kuti angayende wasiwa, nangapenye anthu usiwa wake.) Ndipo anawasonkhanitsira ku malo otchedwa m'Chihebrei Harmagedo. Chibvumbulutso 16:13-16.

[Kabukhuka kachepa kwambiri kuti mulembedwemo zakuya kwambiri za maulosi. Choncho wokawerenga ali yense angapindule kwambiri ngati adadziguwira Bukhu la *Mkangano Wawukuru* (*Great Controversy*) pa mtengo wotsika ndipo pakali pano mabukuwo alipo ochepetsetsa.]

Ambuye akuchenjeza anthu ake ndi mau amphamvu kwambiri m'bukhu limene'li komanso ulosi uwu za momwe Satana wayesetsera ndi kulimbika mtima konye kugwiritsa ntchito machenjere ake ofuna kusokoneza cholinga cha uthenga'wu. Anthu a Mulungu akangokhota pang'ono m'chidziwitso chao naganiza kuti nkondo ya Harmagedo ndi yakukangana kogwiritsa ntchito mfuti pakati pa magulu ankhondo adziko lapansi, pomwepo adzasokonekera osalimvetsetsa bwino tanthauzo leni leni la ulosi'wu. Ulosi uwu ndi uthenga wapadera wa Ambuye kwa anthu ake kuti okonzekere za kulimbana ndi mphamvu za mdima kotsiriza.

Nkhondo 'yoyera' yotsiriza ya dziko lapansi ikufotokozedwa mwakuya kwambiri m'bukhu la Chibvumbulutso.

Chifukwa chiyani bukhu'li linaperekedwa? Yesu Ambuye Wamphamvuyonse (Chibvumbulutso 1:8), "pa Tsiku la Ambuye" (1:10), lomwe ndi loyera lachikumbutso cha chilengedwe chake komanso mphamvu yake yakupulumutsa, analankhula ndi Yohane ndi "mau akuru ngati alipenga, ndi kunena, Ine ndine Alefa ndi Omega, woyamba ndi wotsiriza: chimene upenya lemba m'bukhu nulitumize kwa Mipingo isanu ndi iwiri (1:11). Ine Yesu ndatuma mgelo wanga kukuchitirani umboni za izi m'Mipingo" 22:16). Kwa Yohane kunabvumbulutsidwa zinthu zakuya ndi zochititsa chidwi chachikuru zomwe zidzachitika mu mpingo. Iye anaonetsedwa machitidwe

osiyanasiyana, zoopsa, mikangano ndiponso mapeto a kuombedwa kwa anthu a Mulungu. Zinsinsi zambiri zofunikira zinabvumbulutsidwa kwa iye, makamaka zokhuza utumiki wa mpingo wotsiriza, kuti anthu omwe atembenuke kuchoka ku tchimo aphunzitsidwe za kuopsya kwa zowawa ndi kulimbana komwe kuli patsogolo pao. Pasakhale munthu wosadziwa za zoopsa zomwe zilichitika dziko lapansi. Ngati ziri choncho, nanga, chifukwa chiyani pali kusadziwa kwakuru kokhuza mau ofunikira'wa a Bukhu Lopatulika?

Zotsatira za mphamvu ya kalonga wa mdima ndiyo yakufuna kubisira anthu choonadi chomwe chimaonetsera pambalambanda za machenjere ake. Ichi n'chifukwa chake Khristu Mbvumbulutsi, pozindikira za kuopsa kwa nkondo imene ikuchitika yolimbana ndi kuti anthu asawerenge bukhu la Chibvumbulutso, analankhula kuti, "Wodala iye amene awerenga, kumva, nasunga mau a chinenerocho" (werengani Chibvumbulutso 1:3). Bukhu la Chibvumbulutso linalembedwa kufotokoza za machitidwe onse omwe mpingo wakomana nao ndipo udzapitiriza kutero, mikangano yake ndi maombedwe ake, makamaka okhuza utumiki wa mpingo womalizira ndi "chimaliziro cha maombedwe" a anthu a Mulungu. Tikanamvetsetsa bwino chomwe bukhu'li likutanthauza za moyo wathu, pakanachitika pakati pathu chitsitsimutso chachikuru. Tikuzidwa zakulimbikitsa mwapadera kwa udani umene Satana ali nao pa bukhu la Chibvumbulutso; chifukwa chake n'chakuti mu ili Khristu wabvumbulutsira pambalambanda "machenjerero" a mdaniyo. Komanso kumbali ina bukhu'li likudzwiwitsanso anthu a Mulungu momwe iye akuchitiranso ndi mpingo wake.

Mau oyamba a bukhu la chibvumbulutso akulifotokoza kuti liri: "Chibvumbulutso cha Yesu Khristu" – siliri Chibvumbulutso cha mikangano ya za nkondo za maiko a kum'mawa yomwe ikukhuzanso maiko akum'mawawo, akumadzulo, Russia kapena pfuko lina liri lonse. Ziphunzitsa zotero mukamazimva n'zochokera kwa Satana ndiponso za bodza kotheratu, ndi zopanda umboni wa m'Bukhu Lopatulika. Chibvumbulutso liri "Chibvumbulutso cha Yesu Khristu," ndipo zolembedwa zake zimakhuzanso mpingo wa Khristuyo ndi adani ake.

Mau olankhulidwa "mophiphiritisa" ndi mwa "miyambi" a m'Chibvumbulutso akukhuzanso

mpingo ndi adani ake. Chining'a chomwe chagwiritsidwa ntchito cha Harmagedo, ndi chiphiphiritso cheni cheni ndipo chikukhuza mpingo ndi adani ake.

Satana ali ndi udani waukuru pa ndime izi (Chibvumbulutso 16:12-16) chifukwa ziri chikatikati cheni cheni chakupatsa chidziwitso za chilungamo chakuchitidwa mwa chikhulupiriro, chomwe ndi chofunikira kwa onse amene akufunitsitsa kuima kumbali ya Mulungu woota kuti adutse mu mkangano wotsiriza. Wobvekedwa ndi chilungamo cha Khristu, mpingo udzalowa ndi kulimbana mu mkangano wotsiriza. Limene'li ndilo tanthauzo loona leni leni la Chibvumbulutso 16:13-16. Kumasulira uku kukugwirizana ndi malamulo onse akamasulidwe ka Bukhu Lopatulika. Mwachitsanzo, ndi chodziwika bwino kuti cholinga chomwe Bukhu Lopatulika linalembedwa chinali kufotokoza za mkangano waukuru – kapena chinkhondo – chapakati pa mphamvu za ubwibo ndi kuipa. Mu mkanganowu, mkhristu akuyerekezedwa ngati msilikari yemwe akulimbana ndi mphamvu za mdima atabvala zida zonse za Mulungu, ndi lupanga m'dzanja lake, ndilo Mau a Mulungu – werengani Aefeso 6:10-18. Iye akuuzidwa, "ulimbane nayo nkondo yabwino" (1 Timoteo 1:18), amve zowawa "monga msilikari wabwino wa Khristu Yesu" (2 Timoteo 2:3), ndiponso kulimba "nayo nkondo yabwino ya chikhulupiriro" (1 Timoteo 6:12).

Chibvumbulutso 12:7-9 "nkondo" yaikuru'yi ikufotokozedwa ndipo mathedwe ake akuchulidwa m'ndime 17. Nkhondoyi ikufotokozedwanso mwakuya pa chibvumbulutso 13, pomwe chirombo chinanyamuka ndi kuchita "nkondo" pa oyera mtima mu zaka za Mdima, ndipo bala lake lakuimfa, likupola pogwirizana ndi chirombo cha nyanga ziwiri chomwenso chikufotokozedwa. Pa Chibv. 14 pakufotokozedwa za Uthenga wa Mulungu wakuwakonetsera anthu ake kuti adzathe kudzaima mu nthawi ya mkangano wotsiriza; mutu 15, chinthu chomwe chidzathetsa kulimbana kwa mbali ziwirizi kwa muyaya ndicho mkangano wotsiriza; mutu 16 ukufotokoza mwakuya za mathedwe amkangano wotsirizawo. Pa Chibvumbulutso 17:13-14 zoonjezera zokhuza mkanganowo zikufotokozedwa ndipo pa Chibvumbulutso 19:11-21 ndi mau ena onena mwakuya za "nkondo" yomweyo akuperekedwa, kuphatikiza pa bvumbulutso lina lofotokoza za

mphamvu za tchimo zomwe zakhala zikulimbana ndi Khristu ndiponso mpingo wake.

Yohane atatha kufotokoza za mphamvu imene idzachita zozizwa ndikusonkhanitsira dziko lonse lapansi ku nkondo yaikuru yotsiriza, pa Chibvumbulutso 16, malankhulidwe ophiphiritisa athera pomwepo ndipo liu lokhala ngati kulira kwa lipenga lilankhula mau achilendo osiyana ndi oyambawo akuti, "Taonani, ndidza ngati mbala. Wodala iye amene adikira, nasunga zobvala zake, kuti angayende wasiwa, nangapenye anthu usiwa wake." (Chbv. 16:15).

"Ukapanda kudikira tsono, ndidzafika ngati mbala, ndipo sudzazindikira nthawi yake ndidzazda pa iwe." Chibvumbulutso 3:3. Kubwera kwadzidzidzi kwa Khristu kudzadabwitsa aphunzitsi abodza. Pano iwo atangwanika kuza anthu, "Mtendere ndi mosatekeseka." Monga anachitira ansembe ndi aphunzitsi ku Yerusalemu atatsala pang'ono kuonongedwa, kuti analimbikitsa mpingo ndi mauthenga a mtendere ndi zikondwerero za ulemelero wa dziko lapansi. Iwo akukutenga kukwanitsidwa kwa zizindikilo za nthawi kuti kukusokoneza mtenderewo ndi ufulu wa munthu. Liu la Mzimu Wachinenero likuti chiyani? "Pamenepo chisokonezo chobukapo chidzawagwera" (1 Atesalonika 5:3). Pa onse amene akukhala pa nkhope ya dziko lonse lapansi, pa onse alitenga dziko ili kukhala kwao, tsiku la Mulungu liwafikira monga msampha. Libwera kwa iwo modzidzimutsa monga imachitira mbala usiku.

Dziko lapansi lodzala ndi kuukirana, komanso zisangalalo za umunthu, liri mtulo, lagona m'chitchinjirizo cha uchimo. Anthu akukuyika kubwera kwa Ambuye patali. Akunyozero machenjere onse operekedwa. Akulankhula monyada ndi moyerekedwa, "Zinthu zonse zikhala monga chiyambire chilengedwe." "Mawa kudzakhala monga tsiku lalero, tsiku lalikuru lopera ndithu." 2 Petro 3:4; Yesaya 56:12. Tikhala tikulowerera kwambiri m'chikondi cha zikondwerero. Koma Khristu akuti, "Taonani, ndidza ngati mbala." (Chibvumbulutso 16:15). Pa mphindi ino pamene dziko likufunsa mwamwano, "Liri kuti lonjezanso la kudza kwake?" zizindikilo zikukwanitsidwa. Pamene anthu akupfuula, "Mtendere ndi mosatekeseka," chionongeko chobukapo chifika. Pamene munthu wachipongwe, wokana choonadi wafika podziyenerenza; pamene kuchita malonda opanga ndalama kwafika

posatsatira chilungamo: pamene wophunzira akulakalaka akadakhala ndi chidziwitso osati cha chinthu china chiri chonse koma cha Bukhu lake Lopatulika, Khristu adzafika monga mbala. Chinthu chiri chonse m'dziko lapansi chikugwedezeka. Zizindikiro zonse zikupereka chiopesezo. Zochitika zonse zikuchititsa mdima. Mzimu wa Mulungu ukuchoka ku dziko lapansi, ngozi zikungotsatana ina pa inzake pa nyanja ndi pa mtunda. Kuli anamondwe, zibvomezi, moto wolusa, kusefukira kwa madzi, kuphana kwa mtundu uli wonse. Ndani angathe kulota ziri n'kudza kutsogolo? Chiri kuti chitchinjirizo? Palibe chiri chonse cha umunthu kapena dziko lapansi chingalenjeze za ichi. Mothamanga anthu akuima kumbali imene asankha. Ndi mitima yodzala ndi mantha akuyembekezera ndi kuyang'anitsitsa machitidwe a atsogoleri ao. Koma ngakhale ziri choncho, alipo ena omwe akuyembekezera ndi kuyang'anira ndiponso kugwira ntchito yakukonzekera kudza kwa Ambuye wathu.

Gulu lina liri m'sitima yakupandukira kwakukuru. Owerengeka akukhulupirira ndi mtima ndiponso moyo wao wonse kuti pali gehena yoyenera kuipewa ndi kumwamba koyenera kukhala kwao.

Chisautso chikuyandikira pang'ono ndi pang'ono pa ife. Dzuwa likuturuka ndi kumadutsa mumlengalenga momwe lakhala likuchitira, ndipo miyamba ikupitirirabe kuonetsa ulemelero wa Mulungu. Anthu akupitiriza kudyerera ndi kumwerera, kubzala ndi kumanga, kukwatira ndi kukwatiwa. Amalonda akugula ndi kugulitsa. Anthu akupikisana wina ndi mnzake kufuna kukhala pa maudindo apamwamba. Okonda zokondweretsa munthu akukhamukirabe m'malo a za masewero, ku mabwalo a mpira, mnyumba zosewerera njuga. Chisangalalo chomwe sichinakhalapo chikuchitika, osadziwa kuti pa ora lokhalokhalo lomwe zikuchitika zoterezi chitetzero chikutsekedwa mofulumira, ndipo mlandu wa munthu ali yense uli pafupi kutsirizika kuweruzidwa kwa muyaya. Satana akuzindikira kuti nthawi yake yatsala pang'ono. Iye akugwiritsa ntchito njira zonse za machenjerero ake kusokeretsa anthu, kuwasokoneza, kuwatangwanitsa ndi kuwapusitsa kufikira tsiku lotsiriza pamene miliri idzayamba kutsanulidwa, ndipo mau adzamveka ochititsa mantha kuchokera kumwamba – iye wakukhala wosalungama achitebe zosalungama; ndi munthu wonyansa akhalebe wonyansa; ndi iye wakukhala

wolungama achitebe cholungama; ndi iye amene ali woyera akhalebe woyeretsedwa” (Chibvumvulutso 22:11). Pa nthawi imeneyo mbali ya mwamuna, mkazi ndi mwana ali yense idzakhala itatsimikizika, ndipo chitseko cha chifundo cha Mulungu chidzatsekedwa kwa muyaya. Taonani, ndidza ngati mbala. Wodala iye amene adikira, nasunga zobvala zake, kuti angayende wausiwa, nangapenye usiwa wake. Chibv. 16:15.

Tchimo la mtundu uli wonse lidzachitidwa mopitirira muyeso. Angelo a mdima adzalumikiza mphamvu zao ku za anthu oipa, ndipo monga iwo anazolowera ndikukhala akatswiri pakagwiritsidwe ntchito njira zachipambano kwambiri zosokeretsa ndi zomenyera nkondo ndi kukhala akuchita ichi kwa nthawi yaitali, sadzatheka kugonjera ku kulimbana kotsirizako koma kulimbikitsa nkondo yao ndipo dziko lapansi lonse lidzagawika mbali ziwiri za magulu olimbanawo.

Anthu a Mulungu adzamvetsera mwa chidwi, mau otsimikiza za chisankho chao cha choonadi, ofotozo za chifuniro cha Mulungu kuchokera m'zolemba ndiponso mau a pakamwa. Kuchokera malo ena kufikira ku anzake iwo adzalalikira uthenga wa Mau a Mulungu, kuwapanga amuna ndi akazi kuti achimvetsetse choonadi.

Namondwe wochititsa mantha ndi wopanda chisoni, alinkudza. Kodi takonzeka kukomana naye? Kodi mapazi athu azikika pa Thanthwe? Kodi tiri amodzi ndi Khristu monga iye ali mmodzi ndi Atate?

Yesu anauza ophunzira ake m'munda wa Getsemani kuti “achezere ndi kupemphera.” Koma iye, “nawapeza iwo ali m'tulo.” Iwo sanasamale za chenjezo linaperekedwa mobwerezabwereza'lo. “Chezerani ndi kupemphera.” Koma anaoneka ofoka ndi tulo tomwe akanalimbika mtima kutithetsa akadapitiriza kupemphera kwa Mulungu. Iwo sanaone kufunikira kwa pemphero loona mtima kuti athe kugonjetsa nalo mayesero. Pano, chinthu choipitsitsa monga anachichita Yudasi chatsala pang'ono kubwerezedwa – Satana mwini yekha adzadzionetsera ngati Khristu chinthu chomwe chidzakhala chomalizira chachikuru mu ntchito yake ya kusokeretsa anthu. Kodi Mateyu 24 akutichenjeza motani za ichi? – “Pomwepo munthu akanena kwa inu, Onani, [Iye] Khristu ali kuno, kapena uko musambvomereze [ichi];

“Chifukwa Akhristu onama adzauka,

ndi aneneri onama nadzaonetse zizindikilo zazikuru ndi zozizwa; koterokuti akanyenge, ngati nkotheke, osankhidwa omwe.

“Onani ndakuuziranitu pasanafike. “Chifukwa chake akanena kwa inu, Onani, iye ali m'chipululu; musamukeko. Onani, [Iye] ali m'zipinda; musabvomereze [ichi].” Mateyu 24:23-26.

“Koma inu dikirani nyengo zonse, ndi kupemphera, kuti mulimbike kupulumuka zonse zimene zidzachitika, ndi kuimira pamaso pa Mwana wa munthu.” Luka 21:36

M'kulimbana kotsiriza uku Mkuru wa makamu a nkondo a Yehova (Yoswa 5:15) adzatsogolera kumbali ya khamu la ankondo akumwamba ndi kukhala pakati m'khamulu ndi kutimenyera ife nkondo. Padzabuka mipanduko pakati pathu; tiyembekezera iyi. “Adzaturuka mwa ife, komatu sanali a ife” (werengani 1 Yohane 2:19). “M'mera wonse umene Atate wanga wa Kumwamba sanaubzala, udzazulidwa” (Mateyu 15:13).

Satana, mogwirizana ndi angelo ake komanso anthu oipa, adzayetsa kugwiritsa ntchito mphamvu zao zonse kuti apambane, ndipo adzaoneka ngati akupambanadi. Koma mu mkangano uwu choonadi ndi chilungamo ndizo zidzapambana. Taonani, ndidza ngati mbala. Wodala [Iye] amene adikira, nasunga zobvala zake, kuti angayende wausiwa, nangapenye anthu usiwa wake.

Ndi pophimbidwa ndi chobvala chokhacho chimene Khristu mwini amapatsa pomwe tingayenezedwe kukhala pamaso pa Mulungu. Chobvala ichi, mwinjiro wa chilungamo cha mwini yekha, adzachibveka iye kwa moyo uli wonse wolapa ndi kukhulupirira. “Ndikulangiza iwe,” iye atero, “ugule kwa Ine... zobvala zoyera, kuti udzibveke, ndi kuti manyazi a usiwa wako asaoneke.” Chibvumbulutso 3:18.

Khristu mu umunthu wake anakhala khalidwe langwiro, ndipo ili ndi khalidwe lomwe ali wokonzeka kulipatsanso kwa ife. Chifukwa “Zolungama zathu zonse ziri ngati chobvala chodetsedwa.” Yesaya 64:6. Chinthu chiri chonse chomwe ife timachichita pa tokha chimakhala chodetsedwa ndi tchimo. Koma Mwana wa Mulungu “anaonekera kudzachotsa machimo; ndipo mwa iye mulibe tchimo.” Tchimo likufotokozedwa kuti “ndilo kusayeruzika.” 1 Yohane 3:5, 4. Khristu anakhala womvera chifuniro chiri chonse cha malamulo. Podzifotokoza Mwini yekha anati,

“Kuchita chikondwero chanu kundikonda, Mulungu wanga: ndipo malamulo anu ali m'kati mwamtima mwanga.” Masalmo 40:8. Pamene anali padziko lapansi, anatinso kwa ophunzira ake, “Ine ndasunga malamulo a Atate wanga.” Yohane 15:10. Mwa kumvera kwake kwa ngwiro, iye wachipanga kukhala chotheke kuti munthu ali yense athenso kusunga malamulo a Mulungu. Tikadzikhuthula kwatunthu ife eni kwa Khristu, mtima wathu umalumikizidwa ndi mtima wake, ndipo chifuniro chathu chimaphatikana ndi chake, ndi malingaliro amakhala amodzi ndi ake ndipo maganizo amakhala pansu pa ulamuliro wake; timakhala moyo wa Iye. Ichi ndicho chimatanthauza pakunena kuti kubvekedwa chobvala cha chilungamo chake. Koterokuti pamene Ambuye amatyang'ana ife amaona, osati umaliseche wathu ndi chirema cha uchimo, koma mwinjiro wa chilungamo cha Mwini yekha, womwe ndi kumvera kwa ngwiro kwa malamulo a Yehova.

Oitanidwa ku phwando la ukwati anafufuzidwa ndi mfumu. Oloedwa m'phwandolo ndi okhawa omwe anasunga malamulo ake ndi kubvala chobvala cha ukwati. Umu ndimo zirinso ndi alendo onse oitanidwa ku phwando la uthenga wabwino. Onse anayenera kufufuzidwa mosamalitsa ndi Mfumu yaikuru, ndipo olandiridwa ndi okhawa omwe abvale mwinjiro wa chilungamo cha Khristu.

Chilungamo ndiko kuchita mokhoza, ndipo ndi mwa ntchito zao kuti anthu adzaweruzidwa. Makhalidwe athu amaonetsedwa ndi zomwe tikuchita. Ntchito zimaonetsera chikhulupiriro ngati n'changwiro. Tingathe kulankhula kuti ndi dzina lokhalo la Yesu lomwe munthu angapulumutsidwe nalo pansu pa thambo, koma m'chikhulupiriro kumamkana iye kuti si Mpulumutsi wathu. Choncho sikokwanira kungolankhula mwa mau. Sikokwaniranso kungoganiza kuti tiri ndi chikhulupiriro mwa Khristu ndi kulembetsa maina athu m'bukhu la mpingo. “Munthu amene asunga malamulo ake akhala mwa iye, ndi iye mwa munthuyo. Ndipo m'menemo tizindikira kuti akhala mwa ife, kuchokera mwa Mzimu amene anatipatsa ife.” “Ndipo umo tizindikira kuti timzindikira iye, ngati tisunga malamulo ake.” 1 Yohane 3:24; 2:3. Ichitu ndicho chitsimikizo cheni cheni cha kutembenuka mtima. Kaya kubvomereza kwathu nkotani, koma nkopanda tanthauzo ngati Khristu sangaonetsedwe mu ntchito za

chilungamo.

Choonadi chiyenera kukhazikitsidwa mu mtima. Chiyenera kuyendetsa maganizo ndi kulamulira zofuna za moyo. Khalidwe lonse liyenera kusindikizidwa ndi mau a Mulungu. Kalemba kali konse kapena kansonga ka liu liri lonse la Mulungu kayenera kuonetsedwa m'machitachita a tsiku ndi tsiku. Iye amene afunitsa kukhala ndi khalidwe ngati la Mulungu adzagwirizana ndi muyeso woposawu wa chilungamo cha Mulungu, womwe ndi lamulo lake loyera. Ili liri muyeso umene Mulungu adzayezera nao ntchito za anthu. Ili lidzakhanso loyezera khalidwe pa chiweruzo.

Anthu ambiri amanena kuti mwa imfa ya Khristu lamulo linathetsedwa; koma ndi chiphunzitsa chaocho chikutsutsidwa ndi mau a Khristu mwini wake akuti, "Musaganize kuti ndinadza lne kudzapasula chilamulo kapena aneneri... Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kang'ono kamodzi kapena kansonga kake sikadzachokera kuchilamulo." Mateyu 5:17, 18.

Khristu anadzataya moyo wake ndi cholinga cholikuzanso lamulo lomwe munthu analisawa. Kukanakhala kuti lamulo lina sinthidwa kapena kuchotsedwa panalibe chifukwa chakuti Khristu adzafe. M'kakhalidwe ka moyo wake pa dziko lapansi lye analilemekeza lamulo la Mulungu. Mwa imfa yake analikhazikitsa ilo kukhala langwiro. Iye anapereka moyo wake kukhala nsembe, osati kudzachotsa lamulo la Mulungu, ndi kukhazikitsa muyeso wina wochepera m'chiyero, koma kuti chilungamo chikhale ku nthawi zonse, kuti lamulo lioneke kuti ndi losasinthika, ndi kuti lidzakhala ku nthawi za muyaya.

Ndime 13 mpaka 15 (Chibvumbulutso 16) zikufotokoza za zochitika zomwe zitsogolere kuchionongeko cha Babulo, kuonongedwa kwa magulu omwe akupanga Babulo (magulu atatu – mipingo ndi maulamuliro a za dziko ndiponso chipembedzo cha ziwanda), ndipo mpfundo iyi ikuchitiridwa umboni ndi ndime 15 pomwe Ambuye akuwalankhula anthu ake ndi kuwachenjeza iwo kuti watsala pang'ono kuitseka ntchito ya utumiki wake wa kukhala Mkuruwansembe wathu. Mau okhuza zakufunikira kwakuti munthu asunge, "zobvala zake, kuti angayende wausiwa, nangapenye anthu usiwa wake," akupezekanso pa uthenga wa Ambuye ku mpingo wotsiriza wa chikhristu – werengani Chibvumbulutso 3:18. Uthengawu uli kuitanira kwamsanga kwa Khristu kwa

anthu ake kuti amve za chenjezo lake lakuima pakhomu ndi kugogoda kuti alowe asanasiye lye ntchito yake yakutetezera ndi kubvala chobvala cha ufumu ndi kudza monga MFUMU YA MAFUMU, NDI MBUYE WAAMBUYE, choncho uthenga wa chibvumbulutso 16:15, uyenera kutengedwa kukhala wofunikira kwambiri!

MOTSOGOZEDWA NDI MULUNGU OYERA MTIMA AULALIKIRA UTHENGA WOTSIRIZA KU DZIKO LONSE

"Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwako kwafika, ndi ulemelero wa Yehova wakuturukira. Pakuti taona, mdima udzaphimba dziko lapansi, ndi mdima wa bii mitundu ya anthu; koma Yehova adzakuturukira, ndi ulemelero wake udaoneka pa iwe." Yesaya 60:1, 2. Yehova Mulungu wakumwamba sadzapereka chiweruzo chake chifukwa cha kusamvera ndi kusayeruzika kwa dziko lapansi asanatimize atumiki ake kulichenjeza. Iye sadzaitseka nthawi ya ntchito yake yakutetezera (werengani Chibvumbulutso 22:11) pokhapokhapo uthenga wabwino utalalikiidwa momveka bwino kwa anthu onse. Lamulo la Mulungu liyenera kukwezedwa; ndipo zofuna zake ziyenera kufotokozedwa mwachilungamo, mu njira ya chiyezo, kuti anthu athe kusankha kulilandira kapena kutsutsana ndi choonadi chake. Koma ntchitoyi itsirizika mwachidule ndi m'chilungamo. Werengani Aroma 9:28.

Uthenga wa chilungamo cha Khristu uyenera kulalikiidwa kuyambira kumalekezera ena a dziko kufikira ku malekezera ake ena kukonzetsera njira ya Ambuye. Uwu ndi ulemu ndi ulemelero wa Mulungu, womwe ukutsiriza ntchito ya pa Chibvumbulutso 14:6-12. Uthenga uwu ukugwirizana ndi mauthenga awiri omwe anaperekedwa kale uwu usanaperekedwe. Ukufotokozedwa kuti ukuperekedwa m'mau akupfuula; kutanthauza kuti, ukulalikiidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera:

Ndipo ndinaona mngelo wina alikuuluka pakati pa mlengalenga, wakukhala nao Uthenga Wabwino wosatha, aulalikiire kwa iwo akukhala padziko, ndi kwa mtundu uli wonse ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu;

Ndikunena ndi mau akuru, Opani Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruzo chake; ndipo mlambireni lye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi Nyanja ndi akasupe amadzi.

Ndipo anamtsata mngelo wina mnzake ndi kunena Wagwa, wagwa

Bubulo waukuru, umene unamwetsa mitundu yonse ku vinyo wamkwiyo wa chigololo chake.

Ndipo anawatsata mngelo wina, wachitatu, nanena ndi mau akuru, Ngati wina alambira chirombocho ndi fano lale, nalandira lemba pamphumi pake kapena pa dzanja lake,

Iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasakaniza m'chikho cha mkwiyo wake; ndipo adzazunzika ndi moto ndi sulfure pamaso pa angelo oyerera mtima ndi pamaso pa mwanawankhosa;

Ndipo utsi wa kuzunza kwao ukwera ku nthawi za nthawi; ndipo sapuma usana ndi usiku iwo akulambira chirombocho ndi fano lake, ndi iye ali yense akalandira lemba la dzina lake.

Pano pali chipiro cha oyerera mtima, cha iwo akusunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu. Chvumbulutso 14:6-12

Pano Satana ali mkati mochita zizindikiro zake zonama, koteru kuti nthawi yomwe ya loseredwa m'Chibvumbulutso'yi ikwanitsidwa, ndipo mngelo wamkuru amene adzaliunikira dziko ndi ulemelero wake watsala pang'ono kuyamba kulalikiira za kugwa kwa Babulo, ndi kuitana anthu a Mulungu kuti aturuke kuchoka m'menemo.

M'ntchito yotsiriza yolichenjeza dziko lapansi, kuitanira komveka bwino kudzachitika ku mpingo. Uthenga wa mngelo wachiwiri womwe ndi wakuti, "Wagwa, wagwa Babulo waukuru umene unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake" ubwerezedwa. Ndipo m'mau akupfuula a uthenga wa mngelo wachitatu kudzamvekanso mau ochokera kumwamba akunena, "Turukani m'menemo, anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ake, ndi kuti mungalandireko ya miliri yake; pakuti machimo ake anaunjikizana kufikira m'Mwamba, ndipo Mulungu anakumbukira zosalungama zake." Chibvumbulutso 18:4

Pali ntchito yaikuru yakuti ichtidwe, ndipo makhalidwe onse auzimu woyenera ndi olimbika ayenera kuchitidwa ndi cholinga chomuo netsera Khristu kuti ndi Mpulumutsi wakukhululukira machimo, Khristu wakusenza machimo a dziko, ndiponso Khristu wokhalayo Nthanda, nyenyezi yambanda kucha; tikatero Yehova adzatipatsa chisomo chake pamaso pa onse okhala pa dziko lapansi kufikira ntchitoyi idzatsirizika.

SATANA AKULAKALAKA ATALITENGA UKAPOLO DZIKO LONSE

Chinthu chochititsa mantha kwambiri ndi chomwe Satana akulakalakitse kulikamo dziko lapansi posachedwa.

Pamene uthenga wa chilungamo cha Khristu ukulalikiidwa kuchokera ku malekezera ena a dziko kufikira ku anzake, mphamvu yake idzazunguza mitu onse amene akutsutsana ndi uthengawo.

Sabata lidzapitirira kukhala muyeso waukuru wakuyesera kumvera, ndipo liri kale mbali ya choonadi pomwe mwapadera pakuchitikirapo mkangano. Pamene kuyesedwa za Sabata kotsiriza kudzafika pokakamizidwa pa anthu, pomwepo padzakhala kulekana kwa nthawi zonse pakati pa iwo amene akutumikira Mulungu ndi iwo amene sakutumikira lye.

Maulamuliro a dziko, mogwirizana kulimbana ndi malamulo a Mulungu, adzakhazikitsa lamulo lakuti onse



(Uthengawu ukufalikira dziko lonse. MOSCOW Pamwambapa)

"ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo" (Chibvumbulutso 13:16), atsatiye miyambo ndi maphunzitsa za mpingo posunga sabata labodza. Onse amene adzakana kuchita nao ichi adzapatsidwa dzilango, ndipo kumapeto kweni kweni adzalamulidwa kuti aziphedwa. Pamene gulu la chizindikilo cha kumvera maulamuliro a dziko, lidzalandira lemba la chirombo, gulu lina, pakusankha chizindikilo cha kumvera ulamuliro wa kumwamba, lidzalandira chisindikizo cha Mulungu.

A chipembedzo ndi Olamulira a dziko pano ali mkati kukonzetsera za mkangano ulinkudza posachedwawu. Pofuna kukhala otchuka, ndi kubvomerezeka ndi unyinji wa anthu, aphungu a nyumba za malamulo adzagonjera kumbali ya lamulo la Sunday. Koma iwo amene aopa Mulungu sadzabvomereza za Sunday pozindikira kuti kungotero kudzakhala kuswama Malamulo Khumi a Mulungu. Pa mkangano wa za Sabata'wu padzakhazikikapo mkangano waukuru wotsiriza wapakati pa choonadi ndi chisalungamo. Monga momwe kuzunguridwa ndi ankhondo a chi –



Roma kunali chizindikilo kwa ophunzira a Ambuye kuti kuonongedwa kwa Yerusalemu kwayandikitsitsa, chonchonso kudzakhalala kupandukira kokakamiza kusunga sabata la bodza'li, kuti kudzakhalala chizindikilo chakuti kulekerera kwa Mulungu kwafika pamapeto, ndipo mngelo wa chifundo watsala pang'onong'ono kusiya ntchito yake yakutetezera yomwe sadzaichitanso.

A chipembedzo adzapempha dzanja la mphamvu la olamulira adziko, ndipo mipingo yonse idzagwirizana pa mfundoyi. Gulu lohwimitsa chipembedzo cha Sunday lidzanka likukulirakulira ndi kukhazikika, lamulo lidzakhazikitsidwa lotsutsana ndi onse osunga malamulo a Mulungu.

Iyi idzakhalala nthawi yowawitsa yakuyesa kutsimikizika kwa chisankho chimene munthu anachipanga; – okhawa amene adzakhalala atamvetsetsa ndikugwiritsa ntchito kuitanira kwa Mpulumutsi ku mpingo kwakuti, “mudzitengere zida zonse” za chilungamo chake ndi amene adzalimbike ndi kudutsa mumkangano wotsirizawu. Ndipo pamene namondwe wa chimkanganoyu adzidzayandikira, gulu lalikuru lomwe poyamba linaonetsa ngati likukhulupirira uthenga wa mngelo wachitatu, koma silinapatulidwe mwa uthengawo [mwachitsanzo sanalandira chilungamo chakuchita mwa chikhulupiriro] kudzera pakumvera mau ndi kusunga malamulo a Mulungu, lidzachoka pakati pa anthu a Mulungu

NJIRA YA KUMOYO WOSATHA

ndikukhala limodzi ndi gulu lotsutsa.

Posachedwa anthu a Mulungu adutsa m'mayesero owawitsa, ndipo anthu ochurukitsitsa a iwo amene akuoneka ngati akhristu eni eni a choonadi pano adzakhalala patsogolo kunyansitsa choonadicho. Kuimira choonadi ndi chilungamo panthawiyo lidzakhalala yeso lalikuru ndi chinthu chochititsa mantha. Ndipo kuti iwo adzathe kudutsa chiyesero chomwe chidzakhalala patsogolo pao, afunikira kumvetsetsa chifuniro cha Mulungu munga chikufotokozedwa m'au ake. Okhawa amene moyo wao wakhazikika ndi kutchinjirizidwa ndi choonadi cha Bukhu Lopatulika omwe adzathe kuima osagwedezeka pa mkangano wakuru wotsiriza'wo.

Mkangano waukuru wotsiriza pakati pachoonadi ndi chisalungamo uzakhalala kulimbana kotsiriza kwa nkondo ya mibadwomibadwo yokhuza lamulo la Mulungu. Tikulowa tspano mu nkondo – nkondo yakulimbana pakati pa malamulo a anthu ndi malamulo a Yehova Mulungu.

Chilungamo ndi ulemu zimene lamulo la Mulungu liyenera kuzilandira zidzaonetsedwa ku maiko amene sanachimwepo, patsogolo pa miyamba ya kumwamba ndiponso pamaso padziko la uchimo'li.

Chizunzo chachikuru chikubwera, ndipo pamenepo Ziyoni [oyera mtima] adzachimika, ndikubvala chobvala chake chokongola, iye adzanyezimira kwakukuru nakuonetsa kukongola kwake kokhala m'chiyero.

ZOONJEZERA: PA HARMAGEDO

Pamene mphamvu za maulamuliro amitundu itatuzi zidzachita nkondo ndi mpingo wotsala (Chibvumbulutso 12:17), pakutero iwo adzakhalala “akuchita nkondo pa Mwanawankhosa” (Chibvumbulutso 17:14), uku kudzakhalala kusunkhana ku “nkondo” ya Mwanawankhosa Wamphamvuyonse, amene ndi Mulungu Wamkurukuru, Yesu (Chibvumbulutso 16:14), nkondo yomwe idzathera kuchiongeko (Harmagedo) atanthauza “phiri

laciongeko”) cha adani onse a mpingo wa Mulungu, kuphatikiza anthu onse amene akhala akudzitcha kuti ali akhristu koma sanadzibveka ndi “chobvala cha chilungamo cha Khristu.”

Panopa iwo atangwanika kumachita zozizwa kukweza kukhazikitsidwa kwa chizindikilo cha chirombo; zozizwa izi ndi zomwezomwenso zikuthandizira kulisonkhanitsa dziko lapansi kunkhondo ya Harmagedo.

Ziwanda zikulumikizana ndi chirombo, mneneri wonyenga ndi magulu a chikunja kuti izo zatumizidwa ndi Khristu kunka zikufotokozera munthu ali yense kuti ndi Khristu amene walamulira kuti anthu adzisunga Sunday; izi ndi mphamvu zokhazokhazo zomwe panopa zikulisonkhanitsira dziko lapansi ku Harmagedo.

Pakukhazikitsa lamulo lokakamiza kusunga Sunday, Satana adzakhalala akuchita nkondo ndi “mpingo wotsala.” Lamulo'li pa lokha siliri Harmagedo koma lidzabweretsa chizunzo cha mpingo, ndipo kenaka chakuti oyera mtima'wo adziphedwa. Kuyesera kupha anthu a Mulungu chifukwa chakuti akumvera ndi kusunga Sabata loona chidzakhalala chiyambi cha chiongeko chomwe chidzadza cha Harmagedo. Pakukhazikitsa malamulo okhwima okakamiza kusunga Sunday, kudzakhalala kuchita nkondo kwa Satana pa “mpingo wotsala,” ndipo “Harmagedo” ndi nkondo ya Mulungu (nkondo... ya Mulungu Wamphamvuyonse) yomwe lye adzalowerera pofuna kutchinjiriza anthu ake, ndi kuononga adani a anthu akewo. Harmagedo idzachitika pa iwo amene adzazunza anthu a Mulungu kudzera pakukhazikitsa malamulo okhwima okakamiza kusunga Sunday. Zonse zimene zafotokozedwa pa Chibvumbulutso 16: 17-21 ziri mbali ya “nkondo ya tsiku lalikuru la Mulungu Wamphamvuyonse.” Pano Mulungu akugwiritsa ntchito mphamvu za chilengedwe chake kudzetsa imfa ndiponso chiongeko ku dziko lomwe liri mkati mwakupandukira ndi



kutsutsana ndi anthu ndiponso ulamuliro wake.

“Yehova watsegula pa nyumba ya zida zake, ndipo waturutsa zida za mkwiyo wake” (Yeremiya 50:25).

“Yehova wamakama asonkhanitsa khamu kunkhondo. Achokera m'dziko lakutari, ku malekezero a thambo, ngakhale Yehova, ndi zida za mkwiyo wake, kuti aononge dziko lonse. Kuwani inu; pakuti tsiku la Yehova liri pafupi; lidzafika munga chiongeko chochokera kwa Wamphamvuyonse” (Yesaya 13:4-13).

“Pakuti taonani, likudza tsiku lotentha ngati ng'anjo; ndipo onse akudzikuzana ndi onse akuchita choipa, adzakhalala ngati chiputu; ndi tsiku lirinkudza lidzawayantsa, ati Yehova wa makamu, osawasiyira muzu kapena nthambi” (Malaki 4:1).

“Ndipo ndidzasonkhanitsa zotsala za zoweta zanga za m'maiko onse m'mene ndinazipitikiisiramoo, ndipo ndidzazitengeranso ku makola ao” (Yeremiya 23:3).

“Taonani, chihema cha Mulungu chiri mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nao, ndi iwo adzakhalala anthu ake, ndi Mulungu yekha adzakhalala nao, Mulungu wao.” Chibvumbulutso 21:3. Paradiso adzakhalanso kwao kwa oyera mtima. Alemekizeke Mulungu!

Ndipo ufumu, ndi ulamuliro, ndi ukuru wa maufumu, pansu pa thambo lonse, zidzapatsidwa kwa anthu opatulika a Wam'mwambamwamba; ufumu wake ndiwo ufumu wosatha, ndi maiko onse adzamtumikira ndi kummvera. Danieli 7:27.

Mukafuna kuona, kuwerenga
Kapena Kudinda Mabuku:

www.bible-sabbath.com
www.present-truth.org

www.earthfinalwarning.com
www.worldincrisis.org

www.evolution-facts.org
www.stepstolife.org

MUKAFUNA KUMVA NDI KUDZIWA ZAMBIRI LEMBERANI KU:

Loud Cry and Family Life Ministries
P.O. Box 2850,
Blantyre,
Malawi. Central Africa.

Restoration Seventhday Adventist Ministries
P. O. Box 510751,
Chipata,
Zambia. Central Africa.

Advent Prophecy Update
P.O. Box 70516,
Ndola,
Zambia, Central Africa.